


KUTENGA ZIPATA ZA MDANI

 Mmawa wabwino, aliyense. Ndi wokondwa kukhala titabwerera kachiwiri mmawa uno ku kachisi, kuti tidzapempherere anthu odwala lero. Ndizo, kawirikawiri, ife timayesera kuti tilowe muno, mowirikiza mulimonse, ndi—ndi kudzapempherera anthu amene amabwera muno kuchokera ku malo osiyana, kufuna pemphero.

Ndipo tsopano ife tikhala tikuchoka posachedwapa, tsopano, waku California ndi misonkhano ya ku Gombe la Kumadzulo. Ndipo ife zedi tikupempha mapemphero anu, kuti Mulungu wa Kumwamba akakhale wachifundo kwa ife kumeneko ndi kukatipatsa ife misonkhano yaikululu.

Ndinangolowa muno, dzulo, kapena usiku watha, kani, mochedwa. Ndipo dzulo linali limodzi la . . . Chabwino, tsiku la dzana, ndipo dzulo, linali limodzi la masiku aakulu amalemba ofiira a moyo wanga. Uko, ine ndikudziwa mosachepera anthu awiri, kapena atatu, mu nyumba muno amene anali mboni za kubwera pansu kwa Ambuye, dzulo. Ndi chinthu chachikulu, chodabwitsa chinachitika, chimene ine ndiribe nthawi mmawa uno kuti ndikuuzeni inu. Koma mwina Lamlungu lotsatira mmawa, ife tisananyamuke, ine mwina ndidzakhala nayo nthawi, mu Uthenga, kuti—kuti ndidzakuuzeni inu. Ngati Ambuye alola, ine ndidzakhala kuno, pang'ono pokha kuti ndidzapempherere odwala, Lamlungu mmawa. Ife mwina tingafune kuti tichoke pafupi masana, ngati nkotheke, kupita ku msonkhano waku San Jose mu San Jose, California. Ndipo ngati inu muli nawo anthu aliwonse kozungulira, ku Gombe la Kumadzulo uko. . . Izo ife tikukhulupirira izo zikakhala mwina ora limene ine ndaliyembekezera, motalika kwambiri, kusintha kwa utumiki wanga kubwerapo. Ndipo ziri pafupi kwambiri, ine ndimaganiza kuti izo zikanati zichitike dzulo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti izo zikhala pomwe pano tsopano, ndipo izo zikhala motalikira kupitirira chirichonse chimene ife tinayamba tachiwonapo kapena kuchimva, panobe. Tsopano, inu kumbukirani, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Ndipo chotero ife tikungoyembekezera izo, nthawi iliyonse.

Ndipo ndife oti tikhale ndi msonkhano tsopano ku mabwalo a zionetsero. Ine ndikukhulupirira ndiko kulondola, sichoncho izo, Gene? Ku mabwalo a zionetsero ku San Jose, California. Ndipo iyo idzakhala misonkhano ya masiku khumi, kuyambira pa 20, mpaka 29, ku—ku San Jose. Tsopano, musingotikumbukira ife ndi kumatipempherera ife.

Tsopano ife tiri nayo pafupi, ngati ife titi tituluke mu nthawi, pafupi ora limodzi ndi theka tsopano, pamene ife titi tiyambe

misonkhano yathu ya kupempherera odwala ndi kubweretsa Mawu. Ine ndasankha, mmawa uno, gawo lochepa la Lemba, malo awiri mu Baibulo, kuti ndiyankhulepo.

Koma, ife tisanati tiyankhule, tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa mphindi yokha, kwa pemphero.

² Mulungu wachisomo kwambiri, ife modzichepetsa tikuyandikira mpandowachifumu Wanu wa chisomo mmawa uno, ngati ana osayenera, koma tikubwera ndi chikhulupiriro chosaipitsidwa mwa Mulungu, chimene chinaperekedwa kwa ife ndi Mzimu Woyera, ndi Kukhalapo Kwake kwa nthawizonse ndi ife. Ndi kupyolera mu lonjezo la Ambuye Yesu, kuti ngati ife titati tibwere modzichepetsa ndipo titati tipemphe chirichonse mu Dzina Lake, ife tingati tipatsidwe pempho lathu. Chotero, ife sitiri kuyang'ana mmbuyo pa kuyenera kwathu, chifukwa ife tiribe kulikonse koteroko, koma ife tikuyang'ana mmbuyo ku zoyenera za Gologota, kumene chisomo chathu chinaperekedwa kwa ife mwaulere ndi Mwana wa Mulungu. Ndipo ife timalephera nkomwe kuimitsa misozi yomwe ikanati iyenderere pa mimero yathu, pamene ife tilingalira za ife, anthu osayenera, ndi momwe kuti mwa chisomo Chake paja pa Gologota Iye anatichitira ife izo, kuti ife tikhoze kubweretsedwa pafupi kwambiri kwa Mulungu, ngakhale ku ubale. Ndipo tsopano ife ndife ana aamuna ndi aakazi kwa Iye.

³ Ndipo ife tikubwera mmawa uno, Ambuye, pansi pa denga laling'ono ili, kuti tidzadzipereke tokha, ndi kwa utumiki, kuvomereza machimo athu, ndi—ndi mu kupembedza Kwauzimu. Ife tikudalira kuti Inu mukhala ndi ife ndipo mutipatsa ife kupenya kwamkati kwauzimu kwa kudza Kwanu kwa pafupi, kuti ife tikhoze kukonzeketsera mitima yathu patsiku kwa chochitika chachikulu icho chimene chayang'aniridwa kwa zaka zikwi. Zoonadi chilengedwe chonse chikubuula, kulira kuti chimasulidwe. Ndipo mizimu yathu mkati mwa ife, Ambuye, mowirikiza ikuvomereza, kuti, “If ndife amwendamnjira ndi alendo, ndipo kuno si kwathu, koma ife tikufunafuna Mzinda Womanga Wake ndi Woupanga ndi Mulungu.” Ife tikuyembekezera nthawi yaikulu iyo kuti idze.

⁴ Ambuye, ife tikanakhala osamalitsa kuti misonkhano iyi, pamene ife tasonkhana pano, ife tikupempherera ana Anu amene akudwala ndi osautsika. Ndipo ife tikupempha kuti Inu mukomane nafe lero mwa njira yapadera kwambiri, kuti muchiritse nthenda zonse ndi matenda pakati pathu. Ndipo izo zitakhala, Ambuye, kuti lonjezo ili limene ine ndakhala ndikungoliyankhula mmbuyomu, mu msonkhano ndi Inu uko dzulo, kuwala kwa tsiku kutangotulukira, ndi momwe Inu munatsimikizira izo mobwereza bwereza kachiwiri. Ndipo ife tikumverera kuti ora liri pafupi kwambiri. Ndipo mulole ili likhale tsiku, Ambuye, lomwe ziti zichitike, kuti Inu musintha

utumiki, Ambuye, kupita mu chinachake chimene chiti chikhale chachisomo kwambiri kwa anthu Anu.

⁵ Ndipo tsopano, Atate, Mulungu, ife sitikanati tiwapempherere awa okha pano, koma kwa awo omwe afalikira kudutsa mdziko, amene ali osowa, zonse mwauzimu ndi mwathupi. Perekani kwa iwo, O Ambuye, zokhumba za mitima yawo, chifukwa ana Anu akuvutikira mu masiku ano. Kupsyinja kwa mdani kuli kwamphamvu kwambiri, koma Inu ndinu wamphamvuko. Pakuti izo zinalembedwa, “Wamkulu ndi Iye yemwe ali mwa inu kuposa iye yemwe ali mu dziko.” Mwa ichi ife timagonjetsa. Yankhulani kwa ife kupyolera mu Mawu Anu olembedwa. Ndipo pamene ife tizichoka mmawa uno, mulole ife tizinena monga iwo amene anapita kuchokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula kwa ife mnjira yonse?” Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Yemwe anapereka lonjezo. Amen.

⁶ Ine ndiri kuwerenga tsopano kuchokera ku malo awiri mu Bukhu la Genesis. Ena a iwo akupezeka mu mutu wa 24, kuyambira ndi ndime ya 56, ikuwerengeka monga chonchi.

Ndipo iye anati kwa iwo, Musanditchinge ine ayi, powona kuti Yehova wapambanitsa ulendo wanga; nditumizeni ine kwathu kuti ine ndimke kwa mbuye wanga.

Ndipo iwo anati, Ife timuitana namwaliyo, ndipo timfunsa pa kamwa pache.

Ndipo iwo anamuitana Rebeka, ndipo anati kwa iye, Kodi iwe umka palimodzi ndi munthu uyu? Ndipo iye anati, ine ndipita.

Ndipo iwo anamutumiza Rebeka ndi mlongo wake- . . . mlongo wawo, ndi namwino wake, ndi wantchito wa Abrahamu, . . .

Ndipo iwo anamdalitsa Rebeka, ndipo anati kwa iye, Iwe ndi mlongo wathu, ukhale iwe mai wa zikwi za mamilioni, ndipo lola mbewu yako idzatenge chipata cha iwo amene awada iwo.

⁷ Ndipo mu Genesis 22, ndime ya 15, ife tikuwerenga.

Ndipo mngelo wa YEHOVA anamuitana Abrahamu kuchokera kumwamba nthawi yachiwiri.

Ndipo anati, Pa ine ndekha ine ndalumbira, atero YEHOVA, popeza chifukwa iwe wachita chinthu ichi, iwe suna- . . . sunandikanize mwana wako, mwana wako yekhayo.

Kuti mwa kudalitsa ine ndidzakudalitsa iwe, ndipo mwa kuchulukitsa ine ndidzachelukitsa mbewu zako monga nyenyezi za . . . kumwamba, ndi monga

mchenga . . . pa mphepete ya nyanja; ndipo mbeu yako idzatenga chipata cha mdani wake.

Ndipo mwa mbewu yako mafuko onse a dziko lapansi adzadalitsidwa, chifukwa iwe wamvera liwu langa.

⁸ Tsopano Ambuye atawonjezera madalitso Awo ku kuwerenga kwa Mawu Awo. Tsopano ine ndikanafuna kuti nditenge, ngati iwo ukanati utchedwe mutu, phunziro langa mmawa uno, choyamba, ndi, “Kuyesedwa pa zipata zolonjezedwa.” Ndipo phunziro ndilo: *Kutenga Zipata za Mdani.*

⁹ Mulungu anali akuyiyesa mbadwa, chifukwa Iye anali atamupatsa iye lonjezo. Ndipo pamene Mulungu apanga lonjezo, Iye amafuna kuti akhale wotsimikiza kuti munthu uyu ndi woyenera kwa lonjezolo, Iye asanati akwaniritse chimene Iye ananena kapena chimene Iye alonjeza. Chotero Abrahamu anali atalonjezedwa kuti kupyolera mu mbewu yake dziko lonse likanati lidzadalitsidwe, kuti iye akanadzakhala ndi mwana. Ndipo, mwana uyu, kuchokera mwa iye mukanati mudzabwere Mbewu yomwe ikanati idzadalitse dziko lapansi lonse. Ndipo Abrahamu, pamene lonjezo linaperekedwa kwa iye, anali usinkhu wa zaka sevente-faifi; ndipo Sarah, mkazi wake, anali usinkhu wa zaka sikisite-faifi. Koma Baibulo limatiuza ife kuti Abrahamu sanagwedezeke pa lonjezo la Mulungu, kupyolera mu kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu. Ndipo Mulungu, nthawi ndi nthawi, ankamuyesa iye, koma iye anali atafika ku yesero lotsiriza ilo dalitso lisanati lichitike.

¹⁰ Ndipo ndi momwe izo ziriri ndi Mbewu zonse za Abrahamu. Mulungu amatipatsa ife yesero lotsiriza ilo basi Iye asanati apereke lonjezolo. Ndipo ngati izo zikanakhala zotheka, ine ndikanafuna kuti ndinene chinachake pano, chandekha, koma ine ndichisunga icho. Yesero lotsiriza ilo, kuti awone momwe iwe uti uchitire pa izo. Ndipo pamene Iye anamupatsa Abrahamu yesero ili, Iye anamupeza Abrahamu woona basi monga iye anali pamene iye ankayamba. Dalitso lake lomwe likanati likhale mmawa uno ngati ife amene tikutenga lonjezo Lake la machiritso tikanaima moona basi monga ife tinachitira pamene ife tinaima pano ndi kuzivomereza izo. Ziribe kanthu zomwe adokotala anena, imani moona basi.

¹¹ Ndipo pamene iye anachita izi, ndipo sanamukanize konse mwana wake yekhayo, koma anali pafupi kuti abaye mpeni mu chifuwa cha Isaki, kuti awononge umboni wake. Iye anali atachitira umboni, kuli konse pa dziko lodziwika limene iye anali atadziwana nalo, kuti iye akanati adzakhale ndi mwana uyu. Ndiyeno pamene mwanayo anabwera, iye anafunsidwa kuti atembenuke pawiri, ndi kuti awononge chiyembekezo chokhacho chimene iye anali nacho kuti umboni wake ukwaniritsidwe. Ndipo pamene Mulungu anawona kuti

iyе anali womvera kwa chikhulupiriro icho chimene iye anali nacho mwa Mulungu, Mulungu anayang'ana kuchokera ku miyamba ndipo Iye anati, "Ine ndalumbira pa Inemwini kuti Ine ndikudalitsa iwe ndi kukuchulukitsa iwe, ndipo mbewu yako idzatenga chipata cha mdani wake." Ndi lonjezo bwanji!

¹² Ndipo Rebeka, yemwe anali woti adzakhale mayi wa mwana wodziwika, wolonjezedwa, woyembekezeredwa uyu, pamene iye anaitanidwira ku yesero lotsiriza, la munthu wachirendo yemwe iye anali asanamuwonepo kale. Iye anangowona kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera. Ndipo pamene makolo ake sakanakhoza kulingalira mwathunthu ngati iye anayenera kuti apite ndi mlendo uyu kapena ayi, kuti akakhale mkazi wa mwamuna yemwe anali asanamuwonepo, iye anabweretsedwa ku yesero lotsiriza. "Ife tikamutenga msungwanayo ndipo timulola iye ayankhule. Ife timva kuchokera pakamwa pake ngati iye ati apite, inde kapena ayi."

¹³ Ndi momwe izo zimabweretsedwa kwa Mbewu yonse ya Mulungu. Iyo imayenera kukhala kamwa yako. Mulungu amafuna kuti amve kuchokera kwa iwe.

¹⁴ Chotero pamene iye anaikidwa ku yesero, iye sanadodome konse miniti. Iye anati, "Ine ndipita." Ine ndikuzikonda izo. Osati, "Ndiroleni ine ndipange malingaliro anga. Ndiroleni ine ndiziwerenge izo mobwerezanso." Iye anali atakakamizika kwathunthu. Ndiwo anthu amene Mulungu angakhoze kuwagwiritsa ntchito, pamene iwe wakakamizika kwathunthu kuti Mulungu asunga lonjezo Lake. Anati, "Ine ndipita."

¹⁵ Ndipo anthu ake ndiye, odzozedwa kwambiri, mwina sankadziwa izo, koma iwo ananenera pamene iwo ankaika manja awo pa mlongo wawo, ndi mwana wawo wamkazi; msungwana wokongola, wamng'ono uyu wa Chiyuda, pamene iwo anali kumuika iye pa ngamila ndi kumutumiza iye ku dziko lake lachirendo, pakati pa anthu achirendo. Koma panali Chinachake pa iwo. Iwo anati, "Ukalole mbewu yako ikatenge chipata cha mdani wawo. Ukakhale iwe kholo la zikwi za mamilioni."

¹⁶ Ndipo, lero, mtundu umenewo wa anthu ndi anthu a Mulungu afalikira kuchokera ku nyanja mpaka ku nyanja, kuzungulira mdziko. Mu chiwukitsiro icho iwo adzakhala monga nyenyezi za Kumwamba, pamene kuwala kowala kuja kuzidzatenga malo awo, pamene iwo azidzapita kudutsa mu mlengalenga. Ndipo pamene iwo azidzabwera, iwo adzakhala monga nyanja cham...kapena mchenga mmphepete mwa nyanja. Kudzakhala zikwi za mamilioni a iwo.

¹⁷ "Mbewu yako idzatenga chipata cha mdani wake." Ilo ndi lonjezo lolumbiridwa la Mulungu, "Mbewu ya Abrahamu."

Ndiye, mwa Mzimu Woyera Wake, powona kuti mayiyo amayenera kuti adzakhale gawo la mwana, nayenso, chifukwa

iwo ali gawo la mnofu. Ndiye, Mzimu Woyera ukugwira ntchito kupyolera mwa anthu awa, anati, “Iye. . . Ukalole Mbewu yako ikatenge chipata cha mdani.” Ndiye, Mulungu akulumbira kuti Iye adzatenga chipata cha mdani, ndiye ndi malo anji amene izo zikuwuyika Mpingo wa Mulungu wamoyo?

¹⁸ Ndife Mbewu ya Abrahamu. Pakuti, ife, pokhala akufa mwa Khristu, ife tiri, timatengapo Mbewu ya Abrahamu ndipo tiri olandira ndi iye, pansi pa lonjezo lolumbiridwa lomwelo. Ndife Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira a lonjezo lirilonse limene linaperekedwa kwa iye. Koma pamene mayesero abwera, ndi pamene ife timalephera. Koma ine sindikukhulupirira kuti Mbewu yoonu ya Abrahamu idzalephera. Iwo adzaima molimbika basi ndi omvera monga Abrahamu anachitira.

¹⁹ Tsopano ife tikuwona kuti Mulungu sangakhoze kunena kalikonse kapena—kapena kupanga lonjezo lirilonse kupatula ngati Iye ati adzalikwaniritse ilo. Iye ayenera kuti achite izo polinga kuti akhale Mulungu. Zaka mtsogolomo, pamene anthu omwewa, anthu olonjezedwa, mbewu ya Abrahamu anali pa ulendo wawo, akupita mu—dziko lolonjezedwa, kunali chipata chimene chinaima, ndipo mmwamba momutsutsa iye, ndipo uyo anali m’bale wake yemwe, Moabu, yemwe anati, “Inu simudutsa mdziko langa. Ine ndiwonetsetsa pa izo kuti inu simudutsa mdziko langa.”

²⁰ Iye anati, “Ngati ng’ombe zathu ziti zinyambite uliwonse wa udzu wanu kapena ngati izo ziti zimwe aliwonse a madzi anu, ife tikulipirani inu pa izo.”

Koma iye anati, “Inu simudutsa mdziko lino.”

²¹ Koma lonjezo la Mulungu linagwira moona. Chotero iwo anapita ndipo anakamutenga mneneri wawo, Balaamu, ndipo anamubweretsa iye uko kuti adzawatemberere anthu. Ndipo pano pali zimene iye ananena. Iwo anayesera kumusonyeza iye mbali yoyipa ya mbewu yodalitsidwa, koma Mulungu anamusonyeza iye mbali yabwino yake. Iye anati, “Yense yemwe atemberera Israeli adzakhala wotembereredwa, ndipo yense yemwe amdalitsa iye adzakhala wodalitsidwa.” Ndipo zotchingazo zinasiyidwa ndipo Israeli anadutsa mzigwazo. Mulungu analonjeza kuti iye adzatenga chipata cha mdani wake.

²² Mtsogolomo, mu zaka, kunadza mmodzi dzina lake Daniele, yemwe anali mu mzere wa Mbewu yachifumu iyi, ndi mu mzere wa malonjezo, chifukwa iye anali Mbewu ya Abrahamu. Ndipo Mulungu anali atamusankha iye asanaikidwe maziko a dziko, kuti adzakhale mneneri Wake, ndipo iye anakhala moyo molimba ndipo iye anakhala moyo womvera. Ndipo ngakhale mu dziko lachirendo, iye anali atalinga mu mtima mwake, “Ine sindidzadzziyipitsa ndekha ndi iwo.” Ndiyo Mbewu yeniyeni ya Abrahamu; akukhala mu dziko lomwe linali losiyana, akukhala

pakati pa anthu amene anali osiyana, komabe wolimba ku lonjezo limenelo. “Ine sindidziyipitsa ndekha ndi iwo. Ine ndikhala moona.”

²³ Mulungu anamuika iye ku yesero monga Iye anachitira ndi atate wake, Abrahamu. Ndipo mfumu inati, “Iwe mwina ukhala monga mmodzi wa ife ndi kumapembedza momwe ife timapembedzera, kapena ine ndikuponyera iwe mu khola lodzala ndi mikango yanjala.”

²⁴ Daniele, monga Abrahamu atate ake, anati, “Inu mukhoza kundiponyera ine mu khola la mikango, koma ine sindigwadira kwa lirilonse la mafano anu. Ine sinditenga chipembedzo chanu chachizolowezi. Ine ndikhala woona kwa Yehova.”

²⁵ Ndipo kunafika chiwonetsero ndiye. Mfumu inasunga lonjezo lake ndipo iye anamutenga mneneriyo, kapena anati iye akatengedwe ndipo anaponyedwa mu khola la mikango. Ndipo pamene mikango, mdani wa Daniele, inathamangira kwa mneneri, Mulungu anasunga lonjezo Lake. Iye anatenga chipata cha mdani wake. Mulungu anaimika Mngelo apo patsogolo pa mikango imeneyo, ndipo anatenga chipata. Mulungu amasunga lonjezo Lake. “Iye adzatenga chipata cha mdani wake.” Mulungu ananena chomwecho.

²⁶ Ndiye uko kunali atatu enanso kumusi uko omwe anali atadzilonjeza okha omvera ku chofunikacho, omwe moonadi anali Mbewu ya Abrahamu, ndipo iwo anali Shadireki ndi Misheki ndi Abedenigo, ndipo iwo anaikidwa ku yesero. Ndipo iwo anati, “Ngati inu simugwadira pamene inu mutamva azeze akusewera ndi malipenga akuwomba, ngati inu simugwadira kwa chipembedzo chathu, ndi kuchoka ku zinthu izo zomwe inu muli—muli kuziimira! Ndipo inu nonse ndinu onyowa, mulimonse. Chipembedzo chanu sichiri choposa cha wina aliyense.” Kodi ife sitimazimva izo nthawi zonse? Koma chi—chipembedzo cha Yesu Khristu ndi chosiyana. Mphamvu ya chiwukitsiro Chake ndi yosiyana. Ife ndife anthu osiyana, anthu achirendo, a unsembe wachifumu. Mulungu amapangitsa kusiyanitsako.

²⁷ Koma pamene iwo anati, “Inu muyenera kuti mukhale amodzi a ife.” Zikanakhala ziri zabwino kwa Shadireki ndi Misheki ndi Abedenigo ngati iwowo akanafuna kuti akhale amodzi a iwo, koma iwo sakanati afune kukhala amodzi a akwinawo. Tsopano, iwo anati, “Ngati inu simuchita izo, ife tiri nacho chitseko kunja uko cha ku ng’anjo, imene ife tingakhoze kuitsegula ndi kukuponyerani inu mmenemo, ndipo inu mukhumba mukanakhala amodzi a ife.”

²⁸ Iwo anakumbukira lonjezo. Iwo anawagubisa iwo mpaka kumene ku ng’anjo yamoto. Ndipo pamene iwo anatsegula chitseko ndipo atawaponyera iwo mu malawi, mdani wawo yemwe akanati awathe iwo, iwo anatenga zipata za mdani wawo.

Mulungu anatumiza Mwana Wake mu malawi a moto awo ndipo anaziziritsa mphepo, ndipo ankayankhula ndi iwo pamene iwo anali mmenemo. Lonjezo la Mulungu linagwira moona. Iwo anatenga chipata cha mdani. Anayesedwa choyamba, ndiye iwo anatenga chipata cha mdani.

Kodi sanali Yesu Yemwe anapanga lonjezo? “Ngati inu mubweretsa ngakhale chokhumudwitsa kwa mmodzi wa aang’ono awa, zikanakhala bwino kuti inu mphero imangiridwe pa khosi panu ndipo inu nkuponyedwa mu kuya kwa nyanja. Musati ngakhale muzibweretsa chokhumudwitsa kwa aang’ono awa amene amakhulupirira mwa Ine. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira mwa Ine.”

²⁹ Iye anapanga kusiyantsa. Iye anapanga kusonyeza kwa omwe akanati akhulupirire ndi omwe akanati as akhulupirire.

Kumakhala, nthawizonse, kuli unyinjira utatu wa anthu, uwo ndiwo: wosakhulupirira, wodzipangitsa-kukhulupirira, ndi wokhulupirira. Koma Mulungu ali nayo njira yotsimikizira yemwe ali wokhulupirira. Wokhulupirira uyo amayima zolimba pa zomwe Mulungu anena kuti ndi Choonadi. Inde.

³⁰ Anali Eliya, Mtisibe, pamene zinafika pa chiwonetsero, mpaka iye ankaganiza iye anali mmodzi yekha mu fukolo yemwe anali akukhalirabe moyo Mulungu. Ndipo mfumu inkati imuike iye pa mulandu. Ndipo iwo amuzunza iye. Ndipo mfumukazi yaing’ono ija, yodzilocha utoto, dzina lake Yezebeli, anawopsyeza moyo wake. Ndipo pamene zinafika ku chiwonetsero, Eliya anatenga zipata za mdani wake ndipo anatembenezira fuko lonse kubwerera kwa Mulungu kachiwiri. Mulungu amasunga lonjezo Lake.

³¹ Anali Mose, atakhala nayenso mu mzere wa Mbewu yachifumu iyi, Mbewu ya Abrahamu, kuti pamene iye anatumizidwa uko mu Igupto, kuti akawaombole ana a Israeli; ndipo Mulungu anali atamupatsa iye zizindikiro ndi zodabwitsa kuti akazichite, ndi kuikantha nthaka, ndi kubweretsapo achule, ndi utitiri, ndi mdima, ndi matalala, ndi mvula, ndi moto, ndipo anali atachita zozizwitsa zonse izi. Komabe, pamene iye ankawatsogolera iwo potuluka ndi dzanja la Yehova, uko kunafika nthawi pamene iye anakomana ndi chipata pakati pa iye ndi dziko lolonjezedwa. Uko kunali Nyanja Yofiira, chotchinga pa njira. Iwo anali atazunguliridwa mmenemo ndi ankhondo a Farao, mapiri, ndi zipululu, ndi Nyanja Yofiira. Koma Mose anapita patsogolo ndipo anatenga chipata cha mdani wake, ndipo anawoloka Nyanja Yofiira, nsapato zowuma, pamene iye anali kuyenda pa msewu wafumbi. “Iye adzatenga chipata cha mdani.” Mulungu ananena chomwecho, ndipo izo zikukhazikitsa icho.

³² Zinali zaka pang'ono pokha mtsogolo pamene mayesero anabwera, ndipo mpingo wonse unagwedezeke, monga izo zimakhala zophweka kwambiri kwa anthu osonkhana kuzichita pamene chinachake sichikuwoneka basi kuti chikuchitika mwa njira yomwe icho chimayenera kuti chizikhala chiri. Mulungu amazipangitsa izo mwanjira imeneyo. Mulungu amabweretsa kumangika mu mpingo, “Mwana aliyense yemwe abwera kwa Mulungu ayenera kuyesedwa, ndi kutsimikiziridwa, ndi kuyesedwa.” Iye amalola zodwala zizikukanthani inu. Iye amalola matenda azibwera pa inu, kuti akuyeseni inu ndi kukutsimikizani inu, kuti alitsonyeze dziko kuti ndinu moonadi Mbewu ya Abrahamu. Iye amaloleza izo mwa chifuniro Chake Chomwe. Iye amaloleza ngozi. Iye amaloleza abwenzi kuti akutembenukire mokutsutsa iwe. Iye amaloleza zinthu zonse izi, ndi kumumasula Mdierekezi, kuti akuyese iwe. Ndipo iye adzachita zonse kupatula kutenga moyo wako. Iye akhoza kukuponyera iwe pa bedi ya kusautsika. Iye akhoza kuwatembenezira oyandikana nao mokutsutsa iwe. Iye akhoza kuwutembenuza mpingo kuti ukutsutse iwe. Iye akhoza kuchita pafupi chirichonse, ndipo izo ndi chifuniro cha Mulungu kuti iye achite izo. Iye timaphunzitsidwa kuti izo ndi zofunika kwambiri kuposa golide, kwa ife.

³³ Nanga bwanji Abrahamu ndi Isaki, pa phiri, mmodzi yemwe anapatsidwira lonjezo? Ndipo ndi kumvera kwake ndi kuzindikira kwake, ndi chikhulupiriro chake mwa Yehova, ndi kupyolera mu izo, ndi izo zokha, kuti Mulungu anayang'ana pansu ndipo anati, “Mbewu yake idzatenga zipata. Ine ndalumbira pa Mwiniwanga kuti Ine ndidzachita zinthu izi.” Palibe wina wamkulu yemwe Iye akanalumbirirapo, koma Iye analumbira pa Iyemwini.

Ndiye, ngati Iye anamusiya Abrahamu kuti ayesedwe mpaka pa malo otsiriza aja, Iye ayenera kuti akuyeseni inu ndi ine mpaka ku mphindi yotsiriza iyo, nthawi iyo ya kulingalira pamene chirichonse chimakhala kutali ndi iwe. Iwe umayenera kuima wekha pamenepo. [M'bale Branham akugogoda pa guwa nthawi ziwiri—Mkonzi.] Aleluya! Ndi choncho.

³⁴ Kuima wekha. Kupita kunja uko ndi kuti, “Ngakhale Iye atandipha ine, komabe ine ndizimudalira Iye.” Ndiyo Mbewu ya Abrahamu. Ndiye Mmodzi yemwe amapereka lonjezo. “Ziribe kanthu zomwe ena onsewo azinena, ena onsewo azichita; koma ine ndi nyumba yanga, ife tizimutumikira Mulungu.” Anati, “Ngati ena onsewo ati, ‘Palibe kanthu kwa chowachitikiracho. Ilo ndi gulu la kutentheka’; kwa ine ndi banja langa, ife tizitutumikira Mulungu.”

Ndipo ine ndikanakonda kugwirizana ndi Paulo pomwepa, ndi kuti, “Mu njira yomwe imatchedwa ‘chisokonezo’ momwemo ine ndimamupembedza Mulungu wa makolo athu.”

“Ngakhale mutakhala amanong’onong’o atabwera mu mpingo, ngakhale atakhalapo opotoza, ndipo ngakhale atakhalapo mitundu yonse ya aneneri abodza ndi chirichonse atabwera mu mpingo pakati pa anthu, ndi mwa oyandikana nawo ndi chirichonse; koma kwa ine ndi kwa nyumba yanga, ife tizimutumikira Ambuye. Ngakhale onse awo atasiya kumabwera, ndipo ngakhale mpingo utazizira, osagwirizana; ine ndi nyumba yanga, ife tiziwatumikira Ambuye. Ngakhale ngati wina anapemphereredwa ndipo sanachire; izo ziribe kanthu kochita ndi izo; kwa ine ndi nyumba yanga, ife tiziwatumikira Ambuye.” Zoyesa ndi mayesero.

³⁵ Anthu si osalephera, koma Mulungu ali. Munthu, inu mukaika malingaliro anu pa munthu, iye adzalakwitsa. Mwina osati mwakufuna, koma adzachita izo. Mulungu amamulola iye kuti achite izo chotero kuti Iye akhoze kugwedeza chikhulupiriro chanu kuchichotsa kwa munthu. Chikhulupiriro chathu sichiri mu nzeru ya munthu, koma mu mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu. Ndi pamene Mbewu yona ya Abrahamu imaika lonjezo lake. Chifukwa, iwo angangokhoza kukhala Mbewu ya Abrahamu pamene iwo alandira Mzimu Woyera. Opanda Mzimu Woyera iwo sali Mbewu ya Abrahamu. Chikhulupiriro chomwecho chimene chinali mwa Abrahamu chimabwera mwa wokhulupirira. Ziribe kanthu zomwe zingati zichitike kapena kusiyana kwake, wokhulupirira amayendabe mopitirira.

³⁶ Azondi anabwerera mmbuyo ndipo anati, “O, ndi—ndi zopusa kuti tiyesere. Palibe chofunikira kumapitira mtsogolo konse, chifukwa anthu amenewo ndi zimphona zazikulu chotero kumeneko. Ndipo iwo ali nao maboma aakulu, ndi iwo—iwo ali nazo nthungo, ndi, bwanji, mpakana ife tikuwoneka ngati ziwala pambali pa iwo.”

³⁷ Ine sindikudziwa, koma ine ndiri wokakamizidwa kuti ndizikhulupirira pano kuti Yoswa anali kanjipiti basi kakang’ono, wamng’ono kwambiri basi, kamunthu kakang’ono. Ine ndikukhoza kumuwona iye akudumpha pamwamba, pa—pa china chonga ngati bokosi, ndi kuti, “Amuna ndi abale,” kwa anthu thuu milioni, “ife ndife oposa kukhoza kuti tiwatenge iwo.” Mukuona? Chifukwa? Apo panali Mbewu ya Abrahamu. Mulungu anapereka lonjezo. Icho chinali chotenga chawo. Mulungu anapereka lonjezo. Zinalibe kanthu chomwe otsutsa anali, Mbewu yona ya Abrahamu inati, “Ife tikhoza kulitenga ilo chifukwa Mulungu analipereka ilo kwa ife.”

³⁸ Pamenepo inu mwaima mmawa uno. [M’bale Branham akumenyetsa manja ake kawiri—Mkonzi.] Apo waima Mpingo wa Mulungu wamoyo. Ine sindikusamala zomwe wina aliyense anena, zomwe adokotala anena, chomwe chirichonse, chomwe wosakhulupirira anena, ife tikhoza kuposa kufanizitsa kwa chirichonse chimene chikubwera pa njira. Ife ndife Mbewu ya

Abrahamu, ndipo ife tidzatenga chipata cha mdani wathu, ziribe kanthu chomwe mdani ali. Mulungu anapereka lonjezo. Ilo linali lawo, chokhala nacho chawo.

³⁹ Machiritso ndi chokhala nacho chanu. Chipulumutso ndi chokhala nacho chanu. Mzimu Woyera ndi chokhala nacho chanu. Ndipo alipo alaliki aakulu, zikwi ndi ena otero mu dziko lero, omwe amati, “Izo siziri chomwecho.” Koma Mbewu ya Abrahamu imadziwa kuti izo ziri chomwecho. Iwo amawanda momwemo natenga zipata za mdani. Mulungu anati iwo akanadzatero. Iwo amakhulupirira izo chifukwa ndi lonjezo. “Mbewu yake idzatenga chipata cha mdani.” Tsopano inu mudzapita kupyola kuyesa, mayesero.

⁴⁰ Ndipo Yoswa anaima pajapa, womvera. Munthu wamng'onoyo anati, “Ine sindikusamala momwe aliri aakulu. Ine sindikusamala mtundu wa nthungo yaikulu yomwe ali nayo, momwe makoma awo aliri okwera, ndi momwe izo ziri zazikulu. Lonjezo lathu ndilo, kuti, ‘Chipata chidzatengedwa ndi Mbewu ya ana a Mulungu,’ ndipo ife tikupita kuti tikazitenge izo. Ife ndife oposa kufanizitsidwa ndi iwo.” O, ndiyo Mbewu yowona.

⁴¹ Ambiri a iwo amene anabadwa, mbewu yachibadwa, inati, “Ife sitingakhoze basi kuzichita izo. Palibe chifukwa choti tiziyesera. Mwaona, ife tapitiriridwa chiwerengero. Ife tapitiriridwa kalasi; ife tiri chirichonse.” Ziribe kanthu, iye sakanati. . . Iwo anali kuyang'ana pa, onani, chomwe diso linkaona. Ndipo Yoswa anali kuyang'ana pa zomwe Mulungu ananena.

⁴² Mbewu ya Abrahamu siimayang'ana ku chirichonse cha zinthu zachilengedwe. Iwo amayang'ana ku zomwe Ambuye ananena. Ndilo lonjezo. Bwanji ngati Abrahamu akanati ayang'ane ku zachilengedwe? Pa mkazi wausinkhu wa zaka handiredi. . . Nainte, iye anali. Ndipo iye anali handiredi. Ndipo anali atakhala naye kuchokera ali msungwana wamng'ono, ndipo iye anali mnyamata wamng'ono, ndipo popanda mbewu. Iye sanayang'ane pa zinthu zimenezo. Iye anati anaziwerengera zinthu zimenezo ngati kuti panalibepo, pakuti iye ankaayang'ana kokha ku zomwe Mulungu anati. “Ine ndidzakudalitsa iwe, Abrahamu, ndipo ine ndidzakupatsa iwe mbewu mwa Sarah.” Ndipo iye anakhulupirira izo. Iwe sumayang'ana kwa zotsutsa. Ife timayang'ana pa zomwe Mulungu ananena. Mulungu ananena izo, izo zikukhazikitsa icho.

⁴³ Chotero ndiye pamene iye anafika uko ku Yordani, pamene Yoswa anapangidwa mtsogoleri wamkulu wa ankhondo, ndipo iwo anabwera mpaka ku mphepete komwe kwa madzi ndipo ankakhoza kuyang'ana kutsidya ndi kuwona Yeriko. Koma, pakati pa iwo, pamene Yoswa anali atakonzeketsera ankhondo ake, panali chipata. Chipata chimenecho chinkatchedwa Yordani.

Koma lonjezo la Mulungu ndi labwino pa chipata chirichonse. Ziribe kanthu kuti chipatacho ndi chiani, lonjezo la Mulungu ndi labwino. “Iye adzatenga zipata za mdani wake.” Izo zikukhazikitsa icho.

Pamene iye anafika mpaka ku Yordani mmawa umenewo, mwina, ine ndikuti ndikhulupirire kuti Mdierekezi anali nayo mitambo ya mkuntho itapachikidwa paliponse, madzi a matope aakulu akugudubuzikira mmusi, minda inasesedwa ndi kusefukira. O, ndi nthawi yoyesa bwanji! Koma Yoswa anati, “Konzekani, inu muwuona Ulemerero wa Mulungu.” Ndipo iwo anadzeyeretsa okha ndipo anakhala okonzeka, akukonzeketsa pamene chirichonse chinkawoneka kuti chinali mosiyana. Koma iyo inali Mbewu ya Abrahamu, yemwe Mulungu anamulumbirira, “Ine ndidzamupatsa iye chipata.” Iye anafika ku Yordani, icho chinali chipata chake, ndipo iye anachitenga icho.

⁴⁴ Mmawa wina uwo ine ndidzayenera kuti ndidzafike ku chipata chotsiriza icho nanenso. Inu muyenera kuti mudzafike mpaka ku Yordani, koma Mbewu ya Abrahamu idzatenga chipata. Ziribe kanthu chomwe icho chiri, iye adzatenga chipata cha mdani aliyense.

⁴⁵ Amuna onse awo anali amuna aakulu. Iwo anafera mu mzere. Koma, potsiriza, tsiku lina mu Betlehemu wa Yudea, Mbewu Yachifumu inabadwa. Chimene, ena onse a iwo anali mithunzi chabe. Mbewu Yachifumu inabadwa, osati mwa mwamuna. Koma Iye anabadwa mwa namwali, ali ndi Mphamvu mu mitsempha Yake kuti agonjetse imfa ndi hade. Mulungu anapanga lonjezo. Munthu wamba sakanakhoza kuzichita izo. Koma ngati Mulungu apanga lonjezo, Iye ali basi Mulungu yemweyo yemwe Iye anali maminiti angapo mmbuyomo, ndi Abrahamu, Yehova-yire, Ambuye apereka njira kuti inu mutenge chipata. Ife tichita motani izo? Yoswa anafa. Mose anafa. Ena onse a iwo anafa. Koma Mulungu anati, “Iye adzatenga chipata cha mdani wake.” Kodi iye adzatenga bwanji imfa? Iye ali nayo njira yochitira zinthu. “Iye adzatenga chipata cha mdani wake.”

⁴⁶ Mbewu Yachifumu inabadwa. Iye anayesedwa mu chikhalidwe chirichonse monga ife tiri. Basi monga inu mumayenera kuti muziyesedwa, chomwecho Iye anali. Mdierekezi mwamsanga anamutenga Iye, pamene Iye analandira Mzimu Woyera, anapita mu chipululu kwa masiku forte ndi usiku, kuti akayesedwe. Ndipo pamene Iye anabwerako... Ndipo pa imfa Yake, iwo anakhomerera misomali mu dzanja Lake, ndi kulavulira mu nkhope Yake. Iye anadutsa mu nthenda iliyonse. Koma pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anatsimikizira kuti Iye akhoza kugonjetsa matenda. Pamene amake a mkazake wa Petro anagona chidwalire, ndi manjenje, iye anakhudza dzanja lake ndipo malungo anamuchokera iye. Pamene wakhate anafuula pa chipata,

“Wosayera! Wosayera! Ngati Inu mukulola, Inu mukhoza kundipanga ine wamphumphu.”

⁴⁷ Iye anati, “Ine ndikulola. Khala iwe wamphumphu.” Iye anagonjetsa ndipo anatenga chipata cha khate. Iye anatenga chipata cha malungo.

Iye anapanga chilengedwe chirichonse kumumvera Iye. Iye anali Mbewu ya Abrahamu, Mbewu Yachifumu, Mmodzi yemwe lonjezo linaperekedwako; kwa Iye, Abrahamu ndi Mbewu yonse imene inamutsatira iye, mpaka ku Mbewu Yachifumu, ndi Mbewu yonse ya pambuyo pa Iye. Lonjezo la Mulungu ndi loona. Iye anagonjetsa matenda.

Iye anagonjetsa yesero. Pamene mdani analavulira pa nkhope Yake, kukantha nsagwada Yake, Iye anatembenuzira mbali inayo. Pamene iwo ankamumwetula ndevu pa nkhope Yake ndi kulavulira pa Iye, Iye sanabwezere mwano. Iye anagonjetsa chipata cha mayesero ndi kuchitenga icho.

⁴⁸ Ndiye inu mukuti, “Kupsya mtima kwanga sikungandirole ine kuchita izo.” Inu, Mbewu ya Abrahamu, inde, bwana, Iye anakugonjetserani inu izo.

⁴⁹ Pamene Iye anachitiridwa mwano, Iye sanabwezere mwano. Pamene Iye anatonzedwa, Iye anaugwira mtendere Wake. Pamene Iye anatchedwa mdierekezi, Iye anaugwira mtendere Wake. Iye anali nayo ntchito imodzi, ndipo ndiyo ntchito ya Atate, ndipo Iye ankapita uku ndi uko akuichita imeneyo. Ndiye, potsiriza, iwo anamutengera Iye ku mtanda. Imfa inkayenera kuti ikayang’anizane Naye. Ena onse a iwo anagonjetsa nyanja, ndipo iwo anagonjetsa chilengedwe, ndipo iwo anali atagonjetsa mikango, ndipo iwo anagonjetsa moto. Iwo anagonjetsa chirichonse kupatula imfa. Koma apa panali Mmodzi akumenya mu ubongo Wake, mitsempha Yake, ndipo anali nayo Mphamvu yogonjetsera imfa. Chotero iwo anatenga manja Ake ndipo anamuwongola Iye namukhomera Iye pa mtanda. Iwo anamumenya Iye ndipo iwo anamukwapula Iye mpaka mafupa Ake anakawonekera pa Iye. Koma pamene iwo anatero, ndipo iwo atachita zonse zomwe iwo akanakhoza kuzichita, imfa inamukantha Iye, inati, “Tsopano ine ndikutenga Iwe monga ine ndinamchitira Yoswa. Ine ndikutenga Iwe monga ine ndinamchitira Daniele. Ndipo ine ndichita zonse izi, chifukwa ine ndikupangitsa Iwe kuti ufe.”

⁵⁰ Ndipo Iye anafa mpaka dzuwa linadzichitira manyazi lokha. Iye anafa mpaka chilengedwe chinachita manyazi ndipo icho chinalephera kuti chigwire ntchito. Dzuwa linalowa pakati pa tsiku. Nyenyezi sizikanakhoza kutulukira. Iye anafa mpaka zinthu zinali zakuda kwambiri inu simukanakhoza kuliwona dzanja lanu patsogolo panu, pakati pa tsiku. Ine ndikulingalira chilengedwe chinati, “Ndiloleni ine ndife ndi Iye.”

51 M'bale! Ndiye Mdierekezi anatumiza solo Yake yofunikayo mu maenje opandamalire a hade. Kumeneko zipata zinatseguka, koma Iye anatulukako tsiku lachitatu, ataigonjetsa iyo. Amen. "Mbewu Yake idzatenga chipata cha mdani." Anaigonjetsa imfa! Iye anagonjetsa hade. Mmawa woyamba wa Isitara uja, Iye anawagonjetsa manda. Tsopano ife tikuima, oposa agonjetsi, kupyolera mwa Iye Yemwe anatikonda ife.

52 Pa Tsiku la Pentekoste Iye anatumiza pansu Mzimu Woyera, kuti upitirize, kupyolera mwa Amitundu, kuti ukatengeko Mbewu ya lonjezo. Kutu upereke kwa Amitundu, otayidwa kunjawo, kuti upereke kwa iwo ubatizo wa Mzimu Woyera, kuti ukawabweretse iwo mu Lonjezo. Tsopano ife tiri nawo ufulu kuti tizigonjetsa matenda onse. Iye sitikusowa kuti tiziwagonjetsa iwo; iwo anagonjetsedwa kale. Iye tikungosowa kuti tizitenga lonjezo ndi kupita kukawatenga iwo. Iwo anagonjetsedwa kale. Imfa inagonjetsedwa. Hade inagonjetsedwa. Matenda anagonjetsedwa. Mayesero anagonjetsedwa. Adierekezi onse anagonjetsedwa. Hade inagonjetsedwa. Imfa inagonjetsedwa. Manda anagonjetsedwa. Iye tikuima mu chipata, kumazitenga izo, sitikusowa kuti tiziwombera mfuti. Izo zinalipiridwa kale.

53 Mdani Wake, Iye adzatenga chipata cha mdani wake. Angati? Masauzande a mamilioni. Iye adzagonjetsa chipata cha mdani wake, mdani aliyense. Iye anawuka kwa akufa. Iye tatenga izo chifukwa Iye anazipereka izo kwa ife. Izo zonse ndi mphatso yaulere, pambali pa izo zonse, ndi chirichonse chimene Iye anachita, ndipo anagonjetsa chipata chirichonse. Iye anagonjetsa matenda, anatenga chipata. Chinthu chokha chimene ife tiyenera kuchita ndi kuyenda mpaka ku chipata, ndi kukati, "Mu Dzina la Yesu Khristu, Mgonjetsi!" Amen.

54 Pamene inafika nthawi yoti afe, ndipo imfa inati, "Ndiwoneni ine ndikumupangitsa iye kuti abweze chipembedzo chake."

55 "Mu Dzina la Yesu Khristu waku Nazareti, gudubukira mmbuyo Yordani!" Mbewu ya Abrahamu ikutenga chipata.

56 Chifukwa, Paulo anati, pamene iwo anali kukonzekera kuti amudule mutu wake, Mbewu ya Abrahamu, iye anati, "Imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chiri kuti chigonjetso chako? Mathokozo akhale kwa Mulungu Yemwe amatipatsa ife chigonjetso kupyolera mwa Yesu Khristu."

57 Iye adzatenga chipata cha mdani wake, akuchitenga icho. Tsopano, iye sali kumenyedwa pa chipata. Iye adzagonjetsa icho ndi kuchitenga icho. Iye adzachitenga icho. Izo ziri mu Mphamvu yake yomwe.

58 Mu Mpingo wa Mulungu wamoyo, mmawa uno, mwagona Mphamvu yoti azichiritsa matenda onse. Mu Mpingo wa Mulungu wamoyo mwagona Mphamvu yogonjetsera mayesero onse. Mu zotengedwa ndi Mpingo wa Mulungu wamoyo, mmawa

uno, mwagona Mphamvu yolimanga tchimo ndi kuliponyera ilo kutali, ndi kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, mu Mpingo wa Yesu Khristu.

“Chirichonse chimene inu muchikhumba, pemphani mu Dzina Langa, ndipo icho chidzapatsidwa kwa inu. Kanthawi pang’ono, ndipo dziko (osati Mbewu), (mbewu yosabadwanso) silidzandiwona Ine kenanso. Komabe inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumapeto a dziko.” Chiani? Mbewu Yachifumu. “Ntchito zimene Ine ndikuzichita, inunso muzidzazichita. Ine ndizidzadzitsimikizira Ndekha kuti Ine ndiri ndi inu, pakuti zizindikiro izi zizidzawatsata iwo amene akhulupirira.”

Iye adzatenga mbewu ya mdani wake. Iye adzatenga. Mbewu Yake idzatenga chipata cha mdani wake, ziribe kanthu chomwe chipatacho chiri. Ngati chiri matenda, mayesero, tchimo, chirichonse chipatacho chiri, icho nchogonjetsedwa. Ndipo Mbewu ya Abrahamu imatenga izo.

⁵⁹ Kodi sindinu okondwa, mmawa uno, kumadziwa kuti ife tikuima tsopano oposa mgonjetsi, oposa mgonjetsi? O, palibe kanthu koti tizimenyera. Ndeu yatha. Kherere yawombedwa. Mbendera yakwezedwa. Ndipo mkati mwa mulu wa tchimo uliwonse, mkati mulimonse mwa chipinda cha odwala chirichonse, muli mtanda wokhwekhwerezedwa wakale, utabzalidwa ndi Magazi a Yesu Khristu, Mgonjetsi. Chinthu chokha chimene ife timachita ndi kukhulupirira, kuyang’ana ndi kukhala moyo.

“Ine ndidzakhala ndi inu. Ine ndizidzatsimikizira. Anthu akubwera mu masiku otsiriza, ndi kumati, ‘O, chabwino, izo *zinali*.’ Koma Ine ndidzakhala ndi inu. Ndipo zinthu zomwe zimene Ine ndinkachita, pano pa dziko lapansi, Ine ndidzakhala mwa inu, ndikuchita chinthu chimodzimidzi chomwecho. Ndiye iwo azidzadziwa. Iwo azidzandiwona Ine. A...Anthu Anga azidzandiwona Ine. Mbewu ya Abrahamu izidzandiwona Ine. Iwo azidzandidziwa Ine. Iwo azidzandizindikira Ine. Enawo azidzanditcha Ine, ‘Bezebule,’ basi monga iwo ankachitira. Koma inu muzidzandidziwa Ine, pakuti Ine ndizidzakhala ndi inu. Inu muzidzandiwona Ine, muzidzandiwona ndi diso lanu. Inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndizidzakhala ndi inu, ngakhale mpaka ku mapeto a dziko, zinthu zomwezi zimene Ine ndizikuchita. Iye amene akukhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye azidzazichita nayenso, mtundu womwewo wa ntchito.”

⁶⁰ Ndipo, lero, Mpingo wa Mulungu wamoyo uli nawo mwayi wa kumaima ndi kumawona kugonjetsa, Yesu Khristu woukitsidwa, Mwana wa Mulungu wamoyo, ataima alipo, akukhala moyo mu Mpingo Wake, akuchita chinthu chomwecho

Iye ankachita apo. Ndiye ife tikutenga chipata cha mdani aliyense.

⁶¹ Ngati inu muli naye mdani mmawa uno, ndiye, m'bale wanga, pali kokha... Ngati inu muli Mbewu ya Abrahamu, mutatha kumva izi, kulibe adierekezi okwanira mu gehena amene angakhoze kusunga chipata chimenecho patsogolo pa inu. Icho chitseguka. Ine sindikusamala chimene icho chiri. Inu muziyenda kupita kumeneko, monga Mbewu yolonjezedwa, kuti, "Ine ndikudzitengera ichi chikhale changa. Ichi ndi changa, chifukwa Mulungu analumbira kuti Iye akanadzamuukitsa Yesu, ndipo, kupyolera mwa Yesu, ine ndinagonjetsa. Ine ndikubwera mu Dzina la Mgonjetsi ameneyo, Yesu Khristu. Bwerera mmbuyo. Ine ndikudutsapo." Amen. "Iye adzagonjetsa chipata cha mdani." Ndiye imani pamenepo, ndi mapewa anu mmbuyo ndi chishango chanu chikunyezimira, chitaphimbidwa ndi Magazi a Ambuye Yesu. Mdani azizindikira izo.

⁶² Inu mukakhala nacho chosowa. Yankhulani kwa Iye tsopano pamene ife tikupemphera, inu mkati muno, mmawa uno, pamene inu muli nayo mitu yanu itaweramitsidwa. Ndipo ngati inu muli nacho chosowa, kodi inu mungati mungokweza dzanja lanu kwa Yesu? Ndi kungoziyankhula izo mu mtima mwanu, mu mtima mwanu, ndi kuti, "Ambuye, Inu mukudziwa chosowa changa. Tsopano, ine ndamva, mmawa uno, ndipo ilo ndi Baibulo, 'Iye adzatenga chipata cha mdani.' Ine ndikubwera kudzatenga chipata. Mwina ine ndiri nako kupsya mtima. Mwina ine ndikusowa Mzimu Woyera. Tchimo landimangira ine pansi. Ine ndiri ndi chosowa. Koma ine ndikubwera ku chipata tsopano. Ine ndichitenga icho, mmawa uno, chipata changa. Chotero, perekana njira, ine ndikubwera chodutsa."

⁶³ Ambuye wodalitsidwa, Inu mwaona manja onse awa. Ndipo Inu mukudziwa awa ndi Mawu Anu, Ambuye. Ine ndangowabwereza Iwo, ndipo ndabweretsa pansi kupyola mu Malemba. Makhalidwe a Baibulo, za momwe iwo anagonjetsera maufumu ndipo anachita chirungamo, ndipo anadzimitsa moto, kuwononga kwa moto, ndipo anapuluma nsonga ya lupanga, ndipo anaimitsa kamwa za mikango, ndipo, o, kuwonjezera apo, akazi analandiranso akufa awo kubwerera ku moyo, ndi zinthu zambiri, chifukwa Inu munazilonjeza izo. Ilo ndi lonjezo Lanu, "Mbewu Yake." "Mbewu Yako, Abrahamu, idzatenga chipata cha mdani." Ndipo Inu mumasunga lonjezo Lanu.

⁶⁴ Tsopano perekani kwa iwo, Ambuye, chokhumba cha mtima wao. Mulole iwo apite kuchokera pano munthu wosiyana. Mulole iwo apite, akudziwa kuti iwo ali—iwo ali agonjetsi, chifukwa kuti Mbewu Yachifumu inawagonjetsera iwo. Mfumu Yolemekezeka, pamene Iye anabwera, wobadwa kwa namwali, Iye anagonjetsa mdani aliyense, ngakhale mpaka imfa. Chotero imfa iyoyomwe siingakhoze kuwopsyeza Mbewu ya Abrahamu. Ife tiri nalo lonjezo kuti ife tidzatenga dziko lapansi, ndipo

tidzabwereranso mwa njira yaulemerero kwambiri, mu thupi laumerero, mdani wotsiriza atayikidwa pansu pa phazi, la mwana yekhayo ndi wotsiriza wa Mulungu yemwe ati adzabwere kudzalowa mu Ufumu.

⁶⁵ Ngati alipo awo ali ndi manja awo mmwamba, Ambuye, omwe ali ochimwa, apulumutseni iwo. Iwo amene ali kubwerera mmbuyo, aloleni iwo adziwe kuti iwo sakusowa kuti azikhalabe obwerera mmbuyo. Iye akhoza kutenga chipata icho cha wobwerera mmbuyo. Mwina mmodzi uyo wopsya mtima, lo—loipa, lirime lonyansa, kapena mtima wosilira, kapena wina waliuma, pa ndalama, kapena—kapena chinthu china chonyansa, asiyeni iwo adziwe kuti iwo akhoza kuchitenga chipata chimenecho. Mwina icho ndi matenda, Ambuye, masautso. Iwo akhoza kutenga chipata chimenecho, “Pakuti Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu. Chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ndife agonjetsi, mmawa uno. Perekani izo, Ambuye.

Ndipo pambali pa izo zonse, ntchito yaikulu iyo imene inachitidwa ndi Iye, komabe Iye ali nafe. Komabe, Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita izo. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silimandiwona Ine kenanso, komabe inu muzidzandiwona Ine; pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a m’badwo.” Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mudzipangitse Nokha kudziwika kwa wina ndi aliyense, mmawa uno. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

⁶⁶ Kodi inu mukukhulupirira izo kuti ndi Choonadi? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Mwakachetechete khulupirirani izo kuti ndi Choonadi, popanda kugwadera kumodzi kwa kukaikira mu mtima mwanu. Tsopano ingokumbukirani izi. Kugwira ntchito kwa Mzimu Woyera ndi kophweka kwambiri kuti iko kumawasokoneza amalinaliro aluntha. Zinthu zophweka kwambiri zimene ine ndinayamba . . . Ine ndawuwonapo Mzimu Woyera ukuchita izi. Ine ndimakhoza kunena zinthu zomwe, bwanji, ine sindikanati ndiganize za izo kukhala ziri mwanjira imeneyo. Ngati ine ndikanati ndigwiritse ntchito malingaliro anga omwe, ine ndikanati, “Chabwino, izo sizikanakhoza kukhala zolondola.” Koma izo nthawizonse ndi zolondola. Iye amachita zinthu mophweka kwambiri basi. Ndipo Iye amachita zinthu kuti adzipangitse Yekha kudziwika kwa anthu Ake. Mulungu ali ndi anthu Ake. Iye ali pakati pa anthu Ake. Iye amawakonda iwo. Ndipo Iye akufuna kuti aziwachitira iwo, ndi kumawathandiza iwo; ndi kungowalola iwo kuti azidziwa, osati zomwe Iye *ati adzachite*, koma zomwe Iye wazichita kale. Iye wazichita kale izo. Izo ndi zanu. Izo ndi za inu. Iyo ndi mphatso yaulere yochokera kwa Mulungu Atate wathu, kwa Mpingo Wake.

⁶⁷ Tsopano momwe amalingaliro aluntha ati adzasokonezedwe kwambiri, monga mu masiku a Daniele, ndi mu masiku a ana Achihebri, ndi—ndi ochuluka omwe ife tawakamba mmawa uno. Onani, dziko la aluntha apamwamba mu tsiku lija anali basi olimba kuti agonjetse monga izo ziriri tsopano. Izo nthawizonse wakhala ali mdani, mwa njira yawo yowonera, ndi sayansi yawo yamakono ndi zinthu, zinali basi zosokonezeka ndi zinthu, mwa malingaliro apo, monga zathu ziriri lero. Mwaona, izo zinali chinthu chofanana. Koma kunali awo, nthawizonse, omwe ankayesetsa kukhala pamenepo ndi kumati, “Mulungu akulondola. Mawu a Mulungu ndi owona.”

⁶⁸ Ndipo, inu, inu simukusowa kuti muzigonjetsa, chifukwa Iye anagonjetsa. Chinthu chokha chimene inu muyenera kuti muzichita ndicho kungopita apo ndi kukatenga, kukaima pa chipata, ndi kuti, “Izo ndi zanga. Ichi ndi changa. Mulungu anapereka icho kwa ine, chipulumutso changa. Ngati ine ndikuufuna Mzimu Woyera, Mulungu anawupereka Iwo kwa ine. Lonjezo liri kwa ine, kwa ana athu, onse amene ali akutali komwe, onse ochuluka omwe Ambuye wathu ati adzawaitane.” Ndicho chifukwa ine ndikuima. Basi. . .

⁶⁹ Utumiki wanga, wa kuzindikira za mumtima uku ndi zina zotero, iwo utha posachedwapa tsopano. O, iwo uzikhala nthawizonse ulipobe. Koma iwo posachedwa uthetsa izi, chifukwa iwo ukupita ku chinachake chachikulupo. Mukuona? Iwo ukupitirira mmwamba; kuchokera pa kugwira kwa dzanja, mpaka pa kuzindikira za mumtima, ndipo tsopano iwo ukukonzekera kuti upange umodzi wina. Mukuona? Mwaona izo. Zipenyeni izo ndipo mudziwe kuti ndi zoon. Mukuona? Ine ndikudziwa kuti ndi Choonadi. Ndipo iwo uzipita mokulira, mokwerera, mwabwinoko. Zedi. Chifukwa, Iye analonjeza izo. Ndipo zomwe Iye analonjeza, Iye amazichita. Iye sangakhoze kulephera mu lonjezo Lake. Ndipo izo ndi chiani? Kukhalapo Kwake kwamoyo kwa nthawi zonse ndi ife, kuti alole izo, zikuloleni inu kuti mudziwe kuti Iye wakutengerani inu chipata.

⁷⁰ Iye anali Mbewu Yachifumu. Panalibe wina yemwe akanatenga zipata zimenezo koma Iye. Onse awo mmbuyo umo anali mithunzi ya kudza Kwake. Koma pamene Iye anadza, izo zinatsirizitsa ndeu yonse. Ndeu inathetsedwa ku Getsemene ndi pa Gologota. Ndipo tsopano ife tikungoma, monga agonjetsi. Palibe ndeu yoti tichite. Ife. . .Ndeu yatha. Ife tangokhala nazo izo, chikalata cha umwini chovomerezeka kwa izo. Kudalirika kolembedwa ndi Mulungu, Atate wathu, Yemwe anakweza dzanja Lake, anati, “Ine ndikulumbira pa Inemwini kuti Mbewu yake idzatenga chipata cha mdani.” Ndi izo apo. Icho chinatengedwa kale. “Iye *anavulazidwa* chifukwa cha zolakwitsa zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife *tinachiritsidwa*.” Izo zinachitidwa kale. Iyo ndi ntchito yotsirizidwa. Ife tikungotenga izo. “Ndipo ntchito zimene Ine

ndikuchita, inunso muzidzazichita.” Mfumu ili ndi ife, mmawa uno. Madalitso Ake aakulu, Mzimu Woyera, ukuyenda pa ife. Kuti timverere kumverera kwaulemerero uko, kuti tizidziwa kuti ziri ndendende ndi . . . mu mzere ndi Mawu a Mulungu. Izo zimatipatsa ife chithonhozo chodabwitsa motero, kudziwa kuti—kuti Mulungu ndi Atate athu.

⁷¹ Tsopano, ine ndikukhulupirira, kodi iye—kodi iye anapereka makadi a pemphero mmawa uno? Ine ndinamuza iye, chabwino, ngati uko kukanati kusakhale enanso kungopatula anthu apa kachisi, chabwino, usati ukapereke makadi apemphero aliwonse. Koma ngati uko—uko kukakhala monga teni, anthu fifitini, kapena chinachake, alendo mu zipata, bwanji, apo kaperekeni makadi a pemphero, kuti ife tikakhoze kuwabweretsa iwo apo ndi kuwapempherera iwo. Ndi angati ali alendo ndi ife mmawa uno? Kwezani dzanja lanu. O, mai! Zedi. Alipo fifitini kapena twente a iwo. Chabwino. Ife tiwafoletsa makadi a pemphero awa ndi kuwabweretsa iwo ku nsanja. Mwaona, chifukwa chimene ine ndinanena za anthu apa “kachisi”, iwo amakhala pano.

⁷² Kuzindikira kwa za muntima uku. Kumbukirani, ine ndikuyankhula izi. Kuzindikira za muntima posachedwapa kufika pa mapeto. Padzakhala pali chinachake chachikulu kwambiri ndi chabwino kwambiri, chiri mnjira basi. Analipo, amene ine ndikuwadziwa, ndikuwona inu mukuyang’ana pa abale awiri tsopano, amene anali kuima ndi ine dzulo, pamene izo zinachitika, ndikuona, ndipo dzana, pamene izo zinachitika. Ndipo izo ndi nthawi zitatu motsatana, tsopano, izo zachitika, chitsimikizo kuti izi ziri pakali pano pafupi, mukuona, zikungonzekera kuti zichitike.

⁷³ Tsopano, Ambuye, Inu ndinu Mulungu, ndipo ife ndife antchito Anu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Mawu Anu, chifukwa cha Mzimu Woyera Womwe wadalitsa mitima yathu. Ndipo tsopano ife ndife okondwa. Ife takhala pano, tikudziwa kuti ife ndife agonjetsi. Ife tatenga kale zipata zonse za mdani. Izo zaperekedwa kwa ife, ndipo ife tiri nalo fungulo lotsegula paliponse mu dzanja lathu. Dzina la Yesu Khristu li- . . . tsegula chipata chirichonse cha mdani. Tengani fungulo ili, fungulo la Dzina la Yesu, ndipo li- . . . litsegula chipata chirichonse cha mdani yemwe wakumangirani inu kutali ndi lonjezo lirilonse.

Ndipo, Mulungu, mmawa uno ife tikubwera mu Dzina la Yesu, ndi fungulo ili, kuti titsegule zipata kwa odwala ndi osautsika. Pakuti zinalembedwa mu—mu Mawu Ake, “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda. Iwo adzayankhula ndi malirime atso pano. Ndipo ngati iwo atatenga njoka, kapena atamwa kanthu kalikonse kakupha, iko kasamadzawavulaza iwo. Iwo adzaika manja awo pa odwala ndipo iwo adzachira.” Ife tikudziwa zinthu zimenezo ndi zoonā. Ndipo perekani, mmawa uno, Ambuye, kuti iwo atero, anthu adzakhoze kumaziwona

izo, kupyolera mu mawonetseredwe a Mawu atapangidwa thupi ndipo akukhala pakati pathu, kuti, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwitsa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ndipo mulole iwo avomereze izo ndi kuchiritsidwa, mmawa uno, ku kudwala kwao konse ndi matenda ndi mavuto. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

⁷⁴ Inu tamayimbani, Teddy, *Kungokhulupira*, mwakachetechete ndi mochedwetsa, ngati inu mungatero.

Ndipo chiani? Kodi inu munayambira pa wani? Nambala wani, khadi la pemphero. Wani, thuu, firii, folo, faifi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, kapena chirichonse chimene chiripo. Chabwino. Kodi inu mungatero mwakachetechete, ngati inu mungathe kuimirira, bwerani ku mbali *iyi*.

[Wina akuti, “Kodi inu munaitana angati?”—Mkonzi.] Anha? [Wina akuti, “Ndi zimenezo. Ndi zimenezo.”] Cha . . .

Tiyeni tiwone, nambala wani, nambala thuu. Ndi ndani ali ndi khadi la pemphero nambala wani? [M’bale akuti, “Ine ndiri nayo iyo.”—Mkonzi.] Eya. Nambala thuu. Chabwino, bwana. Nambala firii, nambala foro, nambala faifi, nambala sikisi, nambala seveni, nambala eyiti, nambala naini, nambala teni.

⁷⁵ Pamene iwo akupanga njira yawo ndi kutenga malo awo oti aime, ine ndikufuna kufunsa funso kwa ena a inu. Ndi angati, kodi alipo anthu apa kachisi aliwonse pano, amene akudwala? Anthu apa kachisi, kwezani mmwamba dzanja lanu. Pafupi faifi. . . foro, faifi, sikisi, seveni, eyiti. Eyiti kapena manja naini. Kodi alipo aliyense muno mu kachisi, yemwe sali wa pano pa kachisi, ali alendo ndi ife, ngakhale mukhoza kukhala kuti munabwera muno msonkhano utayamba ndipo simunalandire khadi la pemphero? Kodi mungakweze dzanja lanu? Aliyense yemwe ali nacho chosowa kwa Mulungu, yemwe sali. . . omwe—omwe samabwera ku kachisi uno. Aliyense pano yemwe sali mamembala a kachisi uno, ndi—ndipo komabe inu mukudwala ndipo mulibe khadi la pemphero, mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero? Kodi inu mungakweze mmwamba dzanja lanu, munthu aliyense? Chabwino. Izo nzabwino. Chabwino.

⁷⁶ Tsopano ine ndikuti ndikufunseni inu ngati mungakhale molemekeza basi monga momwe mungathere, kwa basi—maminiti pang’ono okha, ndiyeno ife tiyambira pomwepo ndi kuyamba. Tsopano tiyeni tiwone. Kodi inu mwatsala ndi malo akulu bwanji, M’bale Billy? Chabwino. Kodi uwo uli ndi kuwerengera teni pamenepo? Ine ndinaitana wani mpaka teni.

Leveni, thwelofu, satini, fortini, fifitini, asiyeni iwo aime tsopano. Ngati iwo ali nambala teni, leveni, thwelofu, satini, fortini, fifitini, asiyeni iwo aime. Chabwino. Wani, thuu, firii, foro, faifi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, leveni, thwelofu.

Tikusowa pafupi awiri ena, kuyambira wani mpaka fifitini. [M'bale Branham akuwerenga monong'ona—Mkonzi.] Fifitini, sikisitini, seventini, eyitini, naintini, twente.

⁷⁷ O, dikirani miniti. Ine—ine ndinamuuzza iye kuti angopereka makadi a pemphero kwa anthu omwe sanali apa kachisi. Ndiko kulondola. Mukuona? Chifukwa, izo zikanakhala, mukuona, kuzindikira za mumtima. Anthu amati, “Anthu awa amabwera ku kachisi.” Mukuona? Ine—ine ndikuuzani inu. Ndi angati akhala ali muno. . . sanayambe akhalapo muno kale? Tiyeni tiwone dzanja lanu, palibe yemwe anayamba wakhalapo mu umodzi wa misonkhano yanga kale. Chabwino. Chabwino.

Tsopano, chabwino, mphindi yokha tsopano, M'bale Teddy.

⁷⁸ Tsopano ine ndikhoza kunena izi, kuti, nonse inu mwamvapo za misonkhano, momwe iyo imachitikira, ngakhale, munatero inu, anthu nonse munakhalapo mu misonkhano? Onani? Pamene Ambuye wathu Yesu anali pano pa dziko lapansi, Iye sankadzinenera kuti anali mchiritsi. Iye anali Mbewu ya Abrahamu, ndithudi, ndipo Iye anali nalo lonjezo ndi Iye. Iye anati Iye sankachita kanthu mpaka Atate atamusonyeza Iye. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo Iye anati, “Ine sindingakhoze kuchita kanthu mpaka Atate atandisonyeza ine choti ndichichite.” Ndipo Iye ankaziwona izo mwa. . . Palibe “mpaka Atate *atandiuza* Ine.” “Mpaka Atate *atandisonyeza* Ine.” Yohane Woyera 5:19, “Zimene Ine ndimawawona Atate akuchita, zimenezo amazichita Mwana momwemo.”

⁷⁹ Tsopano pamene Iye—Iye anadza, ife tikupeza, mu kuyamba kwa utumiki Wake, kuti Iye atatenga—mpando wa Davide. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Kuyankhula mwauzimu, a. . .

Pamene Mzimu Woyera unadza pa Iye pa ubatizo, wa Yohane, ndipo Iye anakhala Mesiya wodzozedwa. Tsopano, kumbukirani, Iye anali Mwana wa Mulungu pamene Iye ankabadwa. Iye anali Mwana wa Mulungu wobadwa kwa namwali. Koma pamene Iye anakhala Mesiya, ndi pamene Mzimu Woyera unadza pa Iye, chifukwa *mesiya* amatanthauza “iye wodzozedwayo.” Mukuona? Ndipo Iye anali Iye wodzozedwayo pamene Mzimu Woyera unadza pa Iye. Inu munandimva ine ndikulalikira pa *Mwanawankhosa Ndi Nkhunda*. Ndiye ife tikupeza, pamene Iye. . . Atatha mayesero Ake a masiku forte, Iye anabwerako.

⁸⁰ Ndipo kodi utumiki Wake unayamba chotani, ndi kodi iwo unatha chotani? Ife tikuzipeza izo, mu utumiki Wake kuti kunali munthu dzina lake Andirea, yemwe anapita kuti akamupeze m'bale wake, Simoni, msodzi, ndipo anamubweretsa iye kwa Yesu. Ndipo Yesu anamuuzza iye, anati, “Dzina lako ndi Simoni. Dzina la abambo ako ndi a Yonasi. Kuyambira pano mpakana iwe uzitchedwa *Petro*, lomwe limatanthauza ‘kamwala

kakang’ono.” Inu mukuzikumbukira izo? Ndipo munthu uyu anadabwitsidwa kwambiri pa zomwe Yesu anamuuzza iye!

Tsopano, kodi Mesiya ankayenera kuti azichita izo? Ndi angati akudziwa izo, itini, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni”—Mkonzi.] Iye anali woti akhale Mulungu-Mneneri. Inde, bwana. Mose anati, “Ambuye Mulungu wanu adzautsa Mneneri wonga ine. Izo zidzachitika kuti yemwe sadzamunvera Mneneri uyu adzadulidwa kumchotsa pakati pa anthu.”

⁸¹ Tsopano, ndiye pamene ife tikupeza, kenako, Ake... “Iye anadza kwa Ake Omwe.” Anali ndani amenewo? Ayuda, mwa chibadwa. “Ndipo chotero Ake Omwe sanamulandire Iye ayi,” chotero Iye anali ndiye... Tsopano izo ziyenera kuti zipite kwa Amitundu, mwaona, chifukwa Ake Omwe sanamulandire Iye ayi. “Koma onse amene anamulandira Iye, kwa iwo Iye anawapatsa mphanvu kuti akhale ana a Mulungu.” Chotero tsopano Iye watembenukira kwa Amitundu, ndipo wakhala ali, kwa zaka zikwi ziwiri. Koma tsopano zindikirani zinthu zomwe Iye anachita.

⁸² Ndiye Filipino, iye atawona kale izi zikuchitidwa, iye anapita ndipo anakamupeza Nataniele, ndipo anamuuzza Nataniele yemwe iye anali atamupeza ndi zomwe Iye anazichita. Ndipo izo zinamudodometsa iye. Iye sankakhoza kukikhulupirira izo mokwanira. Koma pamene iye anafika mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, pamene iye anapeza komwe Iye anali, anabwera mu Kukhalapo Kwake, Yesu anati, “Taonani M’israeli mwa yemwe mulibe chinyengo.”

⁸³ Tsopano, ngati inu mukadakhala mutaima pamenepo, inu mukuganiza kuti inu mukanakhala auzimu mokwanira kuti mumvetse Yemwe uyo anali? Inu mukuganiza kuti inu mukanachita izo? Tsopano penyani. Mukuona? Mwamuna uja, Mlendo chabe, nso... uko, Iye mwina akanakhala ali nsodzi. Iye anali mpalamatabwa, ndi chomwe Iye anali. Munthu wopalamatabwa uyu ataima apo, Munthu wausinkhu-wapakati. Ndipo apo panadza munthu uyu. Iye anayang’ana pa iye, monga ena mwa anthu awa pano, anati, “Taonani M’israeli mwa yemwe mulibe chinyengo.” Chabwino, Iye anadziwa bwanji kuti iye anali M’israeli? Si momwe iye anavalira, chifukwa iwo onse ankavala mofanana. “Mwa yemwe mulibe chinyengo.” Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali—munthu wopanda chinyengo?

⁸⁴ Chotero izo zinamudodometsa munthu uyu. Pokhala wokhulupirira weniweni, iye anati, “Rabbi,” kapena m’bale, mlaliki, mphunzitsi, “ndi liti pamene Inu munayamba mwandiwonapo ine?” Mwaona, iye anali kumufunsa Iye.

⁸⁵ Iye anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, ine ndinakuwona iwe.”

Iye anati, “Ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

86 Yesu anati, “Chifukwa ine ndakuuza iwe izi, tsopano iwe ukundikhulupirira Ine? Tsopano iwe uwona zinthu zazikulu zoposa izi.”

87 Ndipo ndicho chifukwa ine ndikukhulupirira kuti Mpingo wa Mulungu wamoyo uwona chinthu chachikulu kuposa ichi. Iwo ukukonzekera kuti uponde mu izo tsopano, mwapafupi, mwaona, chifukwa iwo akhulupirira izo. Iwo amene azikana izo, chifukwa cha zotchinga za chipembedzo, ine ndikukaikira ngati iwo ati adzakhulupirire konse kalikonse. Mukuona? Zinthu . . . Inu mwina muziyenda mu Kuwala kapena mukhala akhungu. Kuwala kumachititsa khungu, kapena mwina kumasonyeza njira.

88 Mbalame zazing’ono, ine ndinazipeza, pa Chosemedwa cha Ufulu. Mutsimikize kuti mukaziwone izo, M’bale Thoms, pamene inu mudzapitako, mwaona. Izo zimamenyetsa maubongo awo, modzigunditsa pamenepo. Ndipo ine ndinati, “Vuto linali chiani?”

89 Anati, “Mmalo motsatira kuwala, mu mkuntho, pomka ku chitetezo, izo zinkayesa kuti zikumenye kuwala kuzime. Izo zinadzipha zokha.”

90 Ndi chinthu chokha chimene chimachitika pamene inu mumenyana nako Kuwala, inu mumadzipha nokha, mwauzimu. Muzingoyenda mu Kuwala pamene Iye ali mu Kuwala, ndiye ife tizikhala nacho chiyanjano wina ndi mzake, mipingo yonse izikhulupirira ndi kumapitirira ndi kumakomedwa nao madalitso a Mulungu. Kodi izo sizikanakhala zodabwitsa?

91 Tayang’anani pa mkazi wa Chisamaria pamene iye anabwera. Iye anali wa Chisamaria, tsopano (osati Myuda), wa Chisamaria. Ndipo Iye anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Ndipo kukambiranako kunapitirira.

Izi ndi za obwera mwatsopano tsopano.

92 Ndipo kukambiranako kunapitirira. Tsopano, iye sankamudziwa Iye pokhala kuti kunalibe Mesiya. Iye anali basi—Mwamuna, Myuda. Mukuona momwe iye ananenera poyamba? Iye anati, “Bwanji, si mwambo wake kuti inu Ayuda muziyankhulana ndi mkazi wa Chisamaria monga chonchi.” Iye anati, “Ife tiribe zochita wina ndi mzake.”

93 Iye anati, “Koma ngati iwe ukanamdziwa Yemwe iwe umayankhula naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa. Ndipo ine ndikanakubweretsere iwe, ndikanakupatsa iwe madzi amene iwe sukanamabwera kuno kumadzatunga.”

94 Bwanji, iye anati, “Tsopano miniti yokha.” Iye anati, “Ife timapembedza mu phiri ili, ndi—ndipo inu Ayuda mumakapembedza ku Yerusalemu.”

95 Yesu anati, “Koma ora likudza pamene—pamene inu simudzasowa kukapembedza konse ku Yerusalemu kapena

m'phiri ili, koma mu Mzimu. Chifukwa Mulungu ndi Mzimu, ndipo iwo amene amupembedza Iye ayenera kumupembedza Iye mu Mzimu ndi Choonadi.” Mukuona? Chabwino, Iye anapitirira, anapitiriza kuyankhulanako mpaka Iye anapeza pamene panali vuto lake. Chiani, inu mukudziwa pamene panali vuto lake? Alipo akudziwa lomwe linali vuto la mkazi wa pa chitsime? Iye anali ndi amuna ochuluka kwambiri, sichoncho iye? Chotero Iye ananena kwa iye, “Pita ukatenge mwamuna wako ndipo ubwere naye kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

⁹⁶ Anati, “Ndiko kulondola. Iwe uli nawo asanu, ndipo yemwe iwe uli naye tsopano si wako.”

⁹⁷ Iye anati, “Bwana!” Tsopano mpenyeni iye. “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.”

Ngati inu mutayendetsa kuwerenga kwa mmalire uko, inu muzipeza izo. “Bwana,” mwa pachiyambi, “Inu ndinu, ine ndazindikira, kuti Inu ndinu Mneneri *ameneyo*.” Kumbukirani, mu Baibulo, ilo limakhala likunena, “Mneneri ameneyo, kodi Inu ndinu ‘Mneneri ameneyo?’” Anali Mneneri uti ameneyo? Yemwe Mose anati akanadzaukapo.

“Ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Tsopano, ife timaphunzitsidwa, ndipo ife tikudziwa pamene Mesiya adzadza, Iye adzachita zinthu izi.” Icho chinali chizindikiro cha Mesiya. Ndi kulondola uko? Kudziwa lomwe linali vuto la iye. Anati, “Ife tikudziwa pamene Mesiya adzadza, Iye adzatiuza ife zinthu izi. Koma Inu ndinu Yani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye, yemwe akuyankhula kwa iwe.”

⁹⁸ Iye anasiya mpoto wake wamadzi. Iye anathamangira mu mzinda, ine ndikulungalira, atangodzigwira mtima wake. Ndi kumati, atagwira manja ake pa chifuwa chake akungodumphu, kumati, “Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Yemwe wandiuza ine zinthu zomwe ine ndazichita. Kodi ameneyu si Mesiya yemwe? Kodi ameneyo si Mmodzi yemwe amene Baibulo linanena kuti akanadzabwera? Ndi Myuda wakhala uko, Munthu wamba chabe, amawoneka ngati mpalamatabwa. Koma Iye wandiuza ine kuti ine ndinali nawo amuna asanu, ndipo inu nonse mukudziwa kuti izo ndi zooni. Ameneyu ayenera kukhala kuti ndi Mesiya.” Si kulondola uko?

⁹⁹ Tsopano, Yesu anati, “Kanthawi pang’ono, kadanga pang’ono ka nthawi, dziko silindiwona Ine aponso. Komabe, inu muzidzandiwona Ine, pakuti Ine ndikhala ndiri ndi inu, ngakhale mwa inu. Ndipo ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita. Ngakhale zochuluka kuposa zimene Ine ndazichita kuno, inu muzidzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate, kubwereranso ku mawonekedwe a Mzimu.”

Nsembe yaperekedwa. Mbewu Yachifumu inafa; Mbewu Yachifumu inawuka kachiwiri. Tsopano Mpingo ukuima wolungamitsidwa, pa kukhulupirira izo, ndipo Mbewu Yachifumu ikhoza kubwera mwa anthu awa ndipo ngakhale nkudzawapanga iwo olowa limodzi, ana aamuna ndi aakazi a Mulungu.

¹⁰⁰ Tsopano, kwa enanu kunjja uko, omwe simuli mu mzere wa pemphero uwu, ine ndinamuza iye kuti angopereka makadi kwa anthu omwe. . . pamene ine ndinamuitana iye mmawa uno. Iye anali atandiitana ine, anati, “Inu mukufuna kuti mupite uko mukapereke makadi ena, adadi?”

¹⁰¹ Ine ndinati, “Ngati kutakhala ochuluka ngati anthu khumi omwe ali akunjja kwa kachisi.”

¹⁰² Tsopano, nthawizina mu kachisi ine ndimaitana ndi kuwapatsa iwo makadi a pemphero. Inu mumabwerera, kuti, “Chabwino, iye amawadziwa iwo. Iwo anali ochokera ku kachisi. Iye amadziwa chikhalidwe chawo. Zedi.”

¹⁰³ Ndiye ine ndinapotoloka, ine ndinati, “Iwo okha amene ali akunjja kwa kachisi, abwere. Chabwino. Inu amene muli akunjja kwa kachisi, inu mukhala amene muti mubwere mu mzere wa pemphero.”

¹⁰⁴ “O, ife sitimawadziwa iwo,” inatero kachisi. “Ife sitikudziwa lomwe liri vuto lawo. Iye akhoza kuti amanama za izo.” Mwaona?

¹⁰⁵ Ndiye ine nkuti, “Palibe yemwe ati abwere. Musiye Mzimu Woyera ungotenga iwo amene ali muno omwe sali ochokera pa kachisi, angokhala kunjja uko.” Komabe, inu basi. . .

¹⁰⁶ Palibe njira nkomwe, yomutengera munthu kwa Mulungu, kupatula iye atakonzedweratu kuti adzakhale mwana wa Mulungu. Palibe basi njira yochitira izo. Yesu anati, “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka Iye.” Ndipo ndicho Choonadi. Chirichonse chimene Iye anachita, panali chinachake chosiyana. “Ngati Iye anazichita izo mwanjira *iyi*, izo zimayenera kukhala mwanjira *iyi*. Ndi njira *iyi*, izo zimayenera kukhala kubwerera mwanjira *iyi*.” Mukuona, ndi kusakhulupirira basi. Koma nzeru imalungamitsidwa ndi ana ake. Chotero, inu, inu mukuona.

¹⁰⁷ Tsopano pano, ine ndikuyesera kuti ndinene kwa—kwa anthu osonkhana awa, ichi, kuti Yesu Khristu anali Mbewu Yachifumu ija. Si ife ayi; ndi Iye. Ife tangokhala olowa a izo, koma zinthu zonse ndi zathu. Bwanji ngati inu mukanaima pamenepo tsiku limenelo pamene Simoni anabwerapo? Ndipo, inu, palibe aliyense. . . Ichi ndi chinthu choyamba chimene Iye anayamba wachichitapo.

¹⁰⁸ Tsopano, icho chikhala chinthu choyamba kwa anthu awa, ngati Iye ati achite icho. Iwo sanayambe achiwonapo icho kale.

¹⁰⁹ Koma pamene Simoni anabwera uko, nsodzi wokalamba, wopanda maphunziro okwanira kuti alembe dzina lake pa chidutswa cha pepala. Baibulo linati iye anali “mbuli ndi wosaphunzira.” *Ndi* ali cholumikizira. Zonse, “mbuli ndi wosaphunzira.” Ndiyeno pamene Iye anayenda nabwera, mu chizindikiro, mphamvu . . . Yesu, Yesu anati, “Dzina lako ndiwe Simoni.” Kodi inu mukuganiza iye anaganiza chiani? Kodi inu mukanati muganize chiani ngati inu mukanakhalabe mutaima pamenepo? “Ndipo dzina la abambo ako ndi a Yonasi. Ndipo kuyambira lero iwe uzitchedwa Petro.” Chiani, inu mukanati muganize chiani? Kodi Munthuyo anali kuwerenga maganizo ake? Chabwino, inu mukanaganiza chiani? Kodi inu mukanaganiza kuti icho chinali chizindikiro cha Mesiya?

¹¹⁰ Ngati icho chiri chizindikiro cha Mesiya mu m’badwo umodzi, icho chiyenera kukhala chiri chizindikiro cha Mesiya, m’badwo wachiwiri, m’badwo wachitatu, m’badwo wachinai. M’badwo uliwonse chiyenera kukhala mofanana, chifukwa Mulungu sangakhoze kusintha. Ndipo ndi angati akudziwa kuti Mesiya anali Mulungu? Zedi. Iye anali Wodzozedwayo. Zedi. Chotero Iye sangakhoze kusintha. Iye ayenera kukhala ali chimodzimidzi.

¹¹¹ Ndicho chifukwa Iye ankayenera kuti achitire umboni chinthu chomwecho kwa Asamaria chimene Iye anachichita kwa Ayuda. Chifukwa, mafuko atatu a anthu ndi Hamu, Shemu, ndi anthu a Yafeti; Ayuda, Amitundu, ndi Asamaria.

¹¹² Tsopano, inu mukuzindikira Mzimu Woyera? Ndi angati akudziwa kuti Petro anali nao mafungulo aku Ufumu? Inu munazindikira, Iye anatsegulira iwo pa Tsiku la Pentekoste, kwa Ayuda. Filipino anapita kumusi ndipo anakalalikira kwa Asamaria, ndipo anawabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu, koma Mzimu Woyera unali usanabwere pa iwo apobe. Iwo anachita kutumiza ndi kukamutenga Petro, yemwe anadzaika manja ake pa iwo ndipo iwo analandira Mzimu Woyera. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo nyumba ya Kornelio, a—Amitundu anaulandira Iwo. Izo zinali zonse za izo. Kuyambira apo mpakana, iwo unaei utangotsegulidwa kwa onse tsopano. Chotero ndi inu apo, mwaona, Iye ankayenera kuti uwutsegulire iwo. Mulungu ali nazo njira zochitira zinthu.

¹¹³ Tsopano, mmawa uno, ngati Mmodzi uyu Yemwe anapereka Lonjezo kwa Mbewu, ndipo ngati mbewu ziri pano . . . ine ndikufuna kuti ndikhulupirire mmodzi aliyense wa inu ndinu. Ngati Mbewu ili pano, zedi Mbewu iliwona Lonjezo. Tsopano, mmodzi aliyense wa anthu awa aima pano akweza mmwamba manja awo, iwo sanayambe konse akhalapo mu misonkhano kale. Iwo ndi alendo kwa ine. Ine sindikumudziwa mmodzi wa iwo. Iwo anangolowa muno. Ndipo maminiti pang’ono apitawo, Billy anawapatsa iwo khadi la pemphero, ndipo pano iwo ayima

pano. Mulipo ochuluka a inu kunja uko, munakweza manja anu mmwamba, omwe munalibe makadi a pemphero, ndipo inu mukadali alendo muno. Izo ziribe chochita chirichonse ndi izo. Inu mungokhulupirira kuti ndinu olandira a lonjezo limenelo. Inu mungokhulupirira kuti ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa. Ndipo mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse, ndipo mumupenye Iye.

¹¹⁴ Chinthu chokha chimene mphatso iyi ili, ndi kungodzipereka wekha kwa Iye. Ine sindimanena kanthu; Iye amakuchita kuyankhulako. Ndipo ngati Iwo uli Mzimu Wake wa uneneri, mneneri nthawizonse ankakhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Izo nthawizonse zimakhala zolondola. Ndipo palibe funso la Chiphunzitso, chifukwa izo ziyenera kumagwirizana ndi Baibulo, ngati ali Mulungu. Mulungu sangakhoze kunena chinachake, ndiyeno nkubwerera pa icho ndi kukachipinda icho mozungulira. Icho chiyenera kumakhala chinthu chofanana nthawi zonse.

¹¹⁵ Tsopano, inu kunja uko, inu mukhulupirire. Ndi zonse zomwe ziri mwa inu, inu mukhulupirire. Tsopano musati musunthe pozungulira kenanso. Mungokhala duu kwenikweni tsopano, aliyense.

Mochedwetsa basi ndi mofewa monga inu mungakhoze.

Izi zachitika kuti, mmawa uno, kuti munthu woyamba waima pano ndi mwamuna. Tsopano ife tikuti titenge Lemba ili.

¹¹⁶ Tsopano kodi inu mukuona pamene ine ndikuima? Ndi angati angakhoze kumvetsa izo? Pano pali amuna ndi akazi aima pano, amene ine sindinayambe ndawaikapo maso, mu moyo wanga. Iwo sanayambe nkomwe akhalapo mu msonkhano wanga, ndipo inu mukuona pamene iwo aima. Iwo sakudziwa chomwe chiti chichitike. Ine sindikudziwa chomwe chiti chichitike. Koma Mulungu analonjeza izo. Abrahamu sankadziwa chomwe chikanati chichitike pamene iye anasolola mpeni kuti amuphe Isaki, koma Mulungu anamulonjeza iye. Ilo linakhazikitsa izo. Iye anali atamulandira iye monga mmodzi wochokera kwa akufa, nkudziwa kuti Iye anali wokhoza kuti amutse iye kwa akufa. Ndi kulondola uko? Chotero izo zikuhazikitsa icho.

¹¹⁷ Tsopano, pano paima mwamuna pafupi nane, ine sindinayambe ndamuwonapo iye, sindikudziwa kanthu za iye. Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ife sitikudziwana wina ndi mzake. Mulungu akutidziwa tonse ife.

Tsopano, mwa mphatso yauzimu, ngati ine ndingakhoze basi mwa mphatso. . . Tsopano, mphatso izo zimabadwira mwa iwe. Mulungu anakonzeratu asanaikidwe maziko a dziko. Ndi angati akudziwa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chotero icho sichikanati chikhale chirichonse chimene ine ndinali nacho, kuti ndiitenge mphatsoyo. Mulungu anangoisankha iyo.

Ine sindinainankhe konse iyo. Iye ainasankha iyo. Mukuona? Monga aneneri a Chipangano Chakale, ndi anthu osiyana, iwo anakonzedweratu kuti adzachite izo, kuti adzachite izi.

¹¹⁸ Tsopano, ngati bamboyu akudwala, ine sindingakhoze kumuchiza iye. Ngati bamboyu ali ndi kusowa, izo zikanadalira pa chimene iye akuchisowa ngati ine ndingamuthandize iye kapena ayi. Zikhoza kukhala, ngati icho chinali chinachake chimzake monga iye... chinachake chaching'ono chimene ine ndingamuthandiziremo nacho iye, bwanji, ine ndikanakhala wokondwa kuti ndichichite icho. Mwina iye ali ndi kupsya mtima. Mwina iye sali nkomwe Mkristu. Mwina iye ndi Mkristu. Mwina iye ndi wonyengezera. Ine sindikudziwa. Bwanji ngati iye ali wongozembera chiwembu, yemwe anazembera muno, ndipo wabwera kuno ndi kumangodzipanga yekha monga chinachake? Mupenye zimene ziti zichitike, mwaona, basi—mungowona zomwe ziti zichitike. Ine sindikudziwa.

¹¹⁹ Koma, onani, inu kuima apa, ndiye inu mukhoza kuima mwangwiro, mukudziwa kuti Mulungu anapanga lonjezo, Mulungu amasunga lonjezo Lake. Mukuona? Tsopano, ngati Mulungu amasunga lonjezo Lake, pakati, pakali pano tsopano, kwa anthu awa; ndi angati kunjwa uko ati akhale kunjwa uko, ndipo ndi mtima wanu wonse muti mukhulupirire izo? Mtima wanu wonse, muti mukhulupirire izo? Ndiye inu mungondikhulupirira ine.

¹²⁰ Tsopano tiyeni tiwone. Tiyeni titenge Lemba. Tsopano, Simoni Petro anabwera kwa Ambuye Yesu. Ndipo pakungofika kwa Ambuye Yesu, Ambuye Yesu anamuuza iye yemwe iye anali, ndi—ndipo anamuuza iye zinthu zokhudza moyo wake. Chabwino, Yesu yemweyo ali moyo lero. Iye... Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye anawuka kwa akufa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira kuti Mzimu wa Umesiya ulimoyo mu Mpingo momwe, lero, mofanana basi monga Iwo unkachitira nthawizonse? [“Ameni.”] Chabwino.

¹²¹ Tsopano, inu mwa omvera, amene mulibe khadi la pemphero, inu muyang'ane mbali iyi ndi kuti, “Ambuye!” Zoonadi, palibe khadi la pemphero mwa omvetsera, ine ndawaimiritsa onse pano. Inu mwa omvetsera munene, “Ambuye, Inu mundigwire ine.” Mufufuze chimene chitachitike. Mupeze chimene chitachitike...?...

¹²² Tsopano, bwana, ngati ikanakhalapo njira mu dziko yokuthandizirani inu, ine ndikanaichita iyo. Mwaona, ine ndine basi, ndife basi alendo pano, ndipo ine—ine ndikukomana nanu kwa nthawi yanga yoyamba. Koma ine ndiri nawo udindo, monga mtumiki, kuti ndizinena Choonadi ndi kuti ndikhale mboni wa Yesu Khristu. Ndipo, tsopano, ine sindikufuna kuti inu mundiuze ine chirichonse. Ine ndikungofuna kuti inu

muzindiyanika ine ngati izo ziri zoonza kapena ayi, ndiyeno mumulole Iye achite izo. Ndipo ngati Iye ati achite mwanjira yomweyo pano pa nsanja, kudzera mu thupi ili, zomwe Iye anachita kupyolera mthupi la Yesu!

Uyo ndi Mulungu, mwa Khristu. Yesu anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate, omwe ali mwa Ine, atandisonyeza Ine. Iye amandiuza Ine choti ndichite.” Chotero sanali Yesu yemwe anamuuza mkazi. Iwo anali Atate, mwa Iye, anamuuza mkazi. Iwo anali—sanali Yesu yemwe anadziwa yemwe Simoni Petro anali, anali Atate amene ankakhala mwa Iye, anadziwa yemwe Simoni Petro anali. Ndi zimenezo. Mukuona? Ndi zimenezo.

¹²³ Ine ndikhoza kukuuzani inu, tsopano, ndinu Mkhristu, inde, bwana, chifukwa inu muli—m—mzimu wokulandira ukunjanja motantha. Ndipo, iye, iye ndi wokhulupirira. Iye ndi Mkhristu. Ndipo inu mukuvutika ndi chikhalidwe cha manjenje zimene zimakupatsani inu vuto la mmimba. [M'bale akuti, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Ndi kulondola uko? [“Ndiko kulondola.”] Mukuona? Mukuona? Tsopano, ndizo ndendende. Zachitika bwanji izo? Ine ndinadziwa bwanji izo. Ndi motani mu dziko momwe ine ndikanadziwira konse izo? Ife sitinayambe taonana wina ndi mzake kale. Ndizo zoonza. Si choncho? [“Ndizo zoonza.”] Mwina Iye akuuzani inu chinachake za inueni. [“Chabwino, ine . . .”] Ine ndikuuzeni inu. Pano pali chinachake. Ine ndikumuwona mkazi pafupi ndi inu. Iye ali ndi inu. Iye ndi mkazi wanu. Iye nayenso akufuna thandizo lina, aponso. [“Ndiko kulondola.”] Inde, bwana. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine pano chimene chiri chovuta ndi akazi anu? [“Ine ndikudziwa Iye akhoza.”] Chabwino, bwana. Iye ali ndi vuto la mtima, zosokonezeka. [“Inde, bwana.”] Ndiko kulondola. Si choncho? Manjenje, naponso. [“Ndiko kulondola.”] Inde, bwana. Tsopano, inu sindinu ochokera mu mzinda uno. [“Ayi, bwana.”] Inu mubwerera kudzera njira *iyi* pamene inu muzipita kwanu, kupita ku Cincinnati. [“Ndiko kulondola.”] Ndiko kulondola. Ndinu ochokera ku Cincinnati, Ohio. [“Inde, bwana.”] Dzina lanu ndinu Milliken. Bwererani, mupite kwanu, mukakhale bwino. Ambuye akakudalitsani inu ndipo inu mukachiritsidwa, inu ndi akazi anu. Mulungu akudalitseni inu.

Bwerani, bwana. Inu mukukhulupirira? Tsopano ingokhalani nacho chikhulupiriro. Musati mukaikire.

¹²⁴ Tsopano khalani molemekeza kwenikweni. Aliyense tsopano mungokhala molemekeza kwenikweni, mukhale chete. Mwaona, Mzimu Woyera ndi wamanyazi kwambiri. Ndi angati amadziwa izo? Wamanyazi kwenikweni basi, Mzimu Woyera, mwaona, basi kusokoneza kulikonse kwakung'ono kumamuvutitsa Iye.

¹²⁵ Malingana ndi madokotala, inu muyenera kufa pompano, ndi vuto la mtima. [M'bale akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Uko

nkulondola. Inu mwabwera kuno kuchokera ku Chicago, Bambo Mosley. [“Inde.”] Dzina lanu loyamba ndi Theodore. [“Inde.”] Inu mukumukhulupirira Mulungu? [“Inde.”] Ndiye pitani kwanu ndipo mukakhale moyo, mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo kakhaleni bwino. Mulungu akudalitseni inu.

¹²⁶ Inu mukumukhulupirira Mulungu? [Mlongo ati, “Zedi ndikutero. Inde, bwana.”—Mkonzi.] Inu mukuvutika ndi chikhaliidwe mu mwendo wanu. Ndinu ochokera kunja kwa mzinda, inunso. [“Inde, bwana.”] Ndinu ochokera ku Owensboro, Kentucky. Dzina lanu ndi Akazi a Lamb. [“Inde, bwana.”] Bwererani kwanu ndipo kapezeni bwino.

¹²⁷ Dona wakhala pomwepoyo, nayenso ndi wochokera ku Owensboro. [Mlongo ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Muli ndi chotupa pa bere lanu apa. Likuyenera kuti likang’ambidwe, mawa. Pitani, mukukhulupirira, ndi kukhala moyo.

¹²⁸ Kodi inu mukukhulupirira, bwana? [M’bale ati, “Inde, ine ndikutero.”—Mkonzi.] Ndife alendo wina kwa mzake. [“Inde, ife tiri.”] Dzina lanu ndi Bambo Gilmore. Ndiko kulondola. Inu mukuchokera ku Anderson, Indiana, kumene kusuntha kwa mpingo wa Mulungu wawukulu uli. [“Ndiko kulondola.”] Ndiko kulondola. Inu mwaima pano chifukwa cha mwana wanu wamkazi wosautsika pang’ono. Iye wapuwala mwagawo. Inu mukukhulupirira? Ndiye zipitani kunyumba ndipo mukampeza iye momwe inu mukukhulupiriramo. Chabwino. Mulungu akudalitseni inu. Khalani ndi chikhulupiriro. Khulupirirani.

¹²⁹ Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, bwana? [M’bale ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ndinu ochokera ku Indianapolis. Ndinu mtumiki wa Uthenga. Uyo ndi mkazi wanu. U-nhu. Iye akuvutika nayenso. [“Ndiko kulondola.”] Iye ali ndi vuto la mu mmero mu mmero. Adokotala. . . Ali ndi vuto la mtima; ndi wamanjenje pang’ono. Ine ndikuwona kuti iye ndi wogontha mu khutu lake. Chiani. . . Bwerani kuno.

Iwe mzimu wa ugonthi, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukulamulira iwe mwa Mulungu wamoyo, tuluka mwa mkaziyo.

Tsopano inu mukukhoza kundimva ine bwino bwino tsopano. Inu nonse mukhoza kupita kwanu ndipo mukakhala bwino. Bwererani ku nyumba kwanu. Inu mukundimva ine, ndipo inu muli bwino. Inu mukakhala bwino.

¹³⁰ Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ingokhalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Khulupirirani.

¹³¹ Nyamakazi yakale iyo ndi zinthu ndi chinthu choyipa mowopsya. Inu mukukhulupirira Mulungu akupangani inu kukhala bwino? Ndiye yendani chotsika kudutsa apo. Pitani kunyumba, mukutamanda Dzina Lake, kumati, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu wokondedwa.”

Chifukwa chimene ine ndinachigwirira icho mwamsanga chotero, mkazi uyu anali ndi chinthu chomwecho, nyamakazi.

Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kukhala bwino? [M'bale ati, "Inde."—Mkonzi.] Chabwino, bwana. Ndiye ingoyendani kudutsa apo, ndi kuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu," ndipo zipitani kunyumba.

¹³² Chabwino, mlongo, ingotembenukani ndi kumabwerera, ndipo mukhulupirire. Inu mwauma mu maondo anu, ndi apa, ndi vuto lanu la mtima, ndi zina zotero. Ingotembenukani ndi kumabwerera kunyumba, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu," ndipo mukakhala bwino. Khulupirani ndi zonse zomwe ziri mwa inu.

¹³³ Inu mukukhulupirira? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Nanga bwanji kunja uko, ena a inu anthu, inu mukukhulupirira? ["Ameni."]

¹³⁴ Dona wamng'ono wakhala apoyo, wa mutu wakuda, muli ndi khunyu, inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kukhala bwino? Inu mukuzirandira izo? Chabwino. Ngati inu mutatero, Iye achita izo.

¹³⁵ Pano pakhala mlaliki, wakhala apa, akufuna kuyenda kwapafupi ndi Mulungu. Sichoncho inu, bwana? Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchitirani inu izo? Kwezerani mmwamba dzanja lanu ndi kuti, "Ine ndikuvomereza izo." A-nha.

¹³⁶ Dona uyu wakhala apa, anaponyera dzanja lake pansu. Iye ali ndi vuto lauzimu lomwe iye akuliganizira. Ndiko kulondola.

¹³⁷ Apa pali dona wamng'ono pano, akudabwa ngati iye ati adzakhale naye mwana wake. Ndiko kulondola. Inu munakhalapo mu umodzi wa misonkhano yanga. Ine ndinakulonjezani inu, mwa Mulungu, mwana. Sindinatero ine? Chabwino. Ndiye pitani kunyumba ndi kukakhala naye iye. Musati muzidandaula za izo panonso.

¹³⁸ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, nonse inu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Aliyense wa inu akukhulupirira? ["Ameni."] Mbewu ya Abrahamu idzatenga chipata, chipata cha mdani. Kodi inu ndinu Mbewu ya Abrahamu, mwa Yesu Khristu? Kwezerani mwamba manja anu ngati inu muli. ["Ameni."]

Ndiye ikani manja anu pa woyandikana nanu, pa woyandikana nanu, pa wina ndi mzake. Ikani manja anu pa wina ndi mzake. Tengani chipata tsopano. Icho ndi chanu. Icho ndi cha inu. "Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala. Mulungu adzawaukitsa iwo." Chabwino, zipempherani mwanjira yanu yanu. Zipempherani momwe inu mumachitira ku mpingo wanu. Ziwapempherani anthu omwe ali ndi

inu tsopano.” Ikani manja anu pa wina ndi mzake ndipo zipempherani.

¹³⁹ Ambuye Yesu, ife tikudza mu Dzina lalikulu ilo, la Wamphamvuzonse wa Mbewu Yachifumu, Mbewu ya Abrahamu, yemwe analonjezedwa Iye pa phiri pamene Inu munapereka mwanawankhosa; ndipo munamuika mwanawankhosa ameneyo mu chipululu, chinthu chozizwitsa, mofanana monga Inu munachitira ndi agologolo aja, dzulo.

Ine ndikupemphera, O Ambuye Mulungu, kuti Inu mutumize Mphamvu, chikhulupiriro. Ndipo mulole Mbewu iliyonse... Ine ndikudziwa kuti iwo atero, Ambuye, chifukwa Inu munati, “Mbewu ya Abrahamu.” Ndipo ngati pakhala pali ena pano omwe akhala akunyengezera kuti ali Mbewu, ndipo asali Mbewu, akhululukireni iwo chifukwa cha cholinga chawo pano, kapena kunyengezera. Ndipo mulole Mzimu Woyera pakali pano uyike moyo wawo pa moto ndi chikhulupiriro chamoyo. Mulole Mzimu Woyera ugweze mu mtima uliwonse ndi kumuchiritsa aliyense pano. Iwo aika manja awo pa wina ndi mzake.

Mbewu Yachifumu inati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo aika manja pa odwala, iwo adzachira.” Ndipo Mmodzi Yemwe anapanga lonjezo alipo pakali pano, akudzisonyeza Yekha kuti Iye ali pano. Apa pali Mbewu ili ndi manja awo pa wina ndi mzake. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Mulole Mzimu Woyera uyenderere kupyolera mwa limodzi lirilonse la manja awo, kupita mu mitima ya anthu, kupita mu matupi, ndi kukachiritsa aliyense yemwe ali mu Kukhalapo Kwauzimu. Perekani izo, Ambuye.

Ine ndikumudzudzula Mdierekezi. Ine ndikudzudzula kusakhulupirira konse. Ine ndikudzudzula mzimu woyipa uliwonse. Ine ndikudzudzula wonamizira aliyense. Ine ndikudzudzula chirichonse chimene chiri chosiyana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo mulole Mzimu Woyera utenge malo Ake mu mtima wa anthu, pakali pano, kupyolera mu chikhulupiriro. Mulole matenda aliwonse ndi nthenda iliyonse, kusautsika kulikonse kuwasiye anthu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁴⁰ Tsopano, Mbewu ya Abrahamu, inu m’badwo wachifumu, ndinu lonjezo, mwa chisomo ndi thandizo la Mulungu, ndi angati a inu mungakhoze kukweza dzanja lanu, kuti, “Ine ndalandira chimene ine ndinachipempha.” Zikomo inu. Ndi zimenezo. Ndi chimene lonjezo liriri. Ndi chimene lonjezo linaperekedwera, kuti inu mukhoze kukhala wolandira zinthu zonse, kupyolera mwa Yesu Khristu yemwe anakupulumutsani inu. Iye anakupulumutsani inu ku tchimo. Iye anakupulumutsani inu ku matenda. Iye anakupulumutsani inu ku imfa. Iye anakupulumutsani inu kwa gehena. Iye anakupulumutsani inu kwa manda.

¹⁴¹ Inu mukuti, “M’bale Branham, koma ife tonse tidzapita mmanda.” Koma manda sangakhoze kutigwira ife. Iye anapita kwa iwo, nayenso, koma iwo sakanakhoza kumugwira Iye. Ndithudi sangakhoze kumugwira Iye.

¹⁴² “Chabwino, M’bale Branham, ine ndikuyesedwa kwambiri.” Iye anali, nayenso. Koma Iye anakupulumutsani inu ku mayesero.

¹⁴³ “Musatitsogolere ife kokatiyesa, koma mutiombole ife kwa woipayo.” Mwaona, Iye anazichita izo. Izo zonse ndi zanu. Chirichonse ndi chanu, kupyolera mwa Yesu Khristu. Iye amakupatsani inu chirichonse, mwaule. Palibe malipiro kwa izo, ngakhale kanthu. Izo ndi zanu basi pakali pano. Kodi sindinu okondwa nazo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi sindinu okondwa chifukwa cha Iye? [“Ameni.”] Mathokozi akhale kwa Mulungu.

¹⁴⁴ Tsopano, pakhala pali misonkhano, usiku uno. Inde. Ndi usikuuno, hafu pasiti seveni usikuuno. Ine ndiwalola abusa kuti akuuzeni inu. Bwerani. Bwerani.

Tsopano, Lamlungu lotsatira mmawa, Ambuye wabwino akalola, ine ndidzabwerera kuti ndidzapempherere odwala, ku kachisi, kapena kulikonse.



KUTENGA ZIPATA ZA MDANI CHA59-1108
(Possessing The Enemy's Gates)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Novembala 8, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2000 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2000 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org